

# *KUZINDIKIRA TSIKU LANU*

## *NDI UTHENGA WAKE*



Moni wa m'mawa abwenzi. Tiyeni tikhalebe chiimire kwa kamphindi.

Mulungu wokonedwa, pamene ife m'moyo uno wolimbana tapuma, kwa mphindi zochepa zikudzazi kapena ora, chirichonse chimene Ine mwatipatsa, tipereka matamando ndi ulemerero kwa Inu, kulalikira Mawu Anu, kukudziwani inu koposa, . . . Ndi chifukwa chake tasonkhana m'mawa uno. Ndipo tikukuthokozani, Mulungu, chifukwa pali anthu amene akhozeka ndipo adzikhonzekera okha kubwera kudzamvetsera. Mosamalira m'mene zinthu zakhalira ndi nthawi ndi - imene tikukhalamo, akukhulupirirabe. Ndipo tikukuthokozani chifukwa cha iwo.

<sup>2</sup> Mulungu, tikuthokoza kwa Inu chifukwa cha mphamvu Yanu yaikuru ya machichiritso, malonjezano a Mawu Anu. Mitima yathu ikuyaka pamene tikumva maumboni awa. Kuzunzika kwa mitundu yonse kumene kwaikidwa pa ana a amuna a anthu, Inu ndi chisomo chanu ndi mphamvu ndi lonjezano Lanu zawachiritsa iwo. Ndipo ali pano kuchitira umboni, kupereka ulemerero kwa Mulungu. Tikukuthokozani chifukwa cha ichi. Ndipo tsono, mutilole ife timve uthenga umene mwatipatsa ife ora lino. Pamene tiwerenga mu Mawu Anu mutipatse ife thandauzo la chimene ife tawerenga. Mulole chifuniro chanu chichitike mu zonse. Pakuti tikupempha ichi mu Dzina la Yesu. Amen. (Mukhoza kukhala pansu.)

<sup>3</sup> Ndi chamwayi kukhala pano m'mawa uno. Ndiri wokondwa ndi inu nonse. Ndipo Mbale Wood, Mbale Roy Roberson, abale ambiri, agwira ntchito yao mokhulupirika kuika chopereka mpweya wabwino m'nyumba ino pa cholinga chimenechi, chifukwa lamulungu lapaitalo anaona m'mene munabvutikira. Ndipo anali ndi tindalama mu thumba la mpingo, kotero anakagwira ntchito ndi kugwiritsa ntchito kuti inu mukhale mofewa, ndi ndalama zomwe munaika mu chopereka, ku - pamene mungakhale ndi kumvera uthenga. Ndi kozizirirapo lero kuposa m'mene kunakhalira. Kotero tikuthokoza kwa Mulungu ndi kwa inu anthu chifukwa cha mwayi umenewu.

<sup>4</sup> Ndiri wokondwa Mbale Roy Borders. . . Anafuna kukhala kumbuyoko m'mawa uno. Kotero ndinamuuzwa kuti atenge mpando wake akhale kuno ndi atumiki awa, koma sanakhoze kuchita chimenecho. Monga nonse mukudziwa, Mbale Borders

amatiimirira ife kunja kwa malo ano. Ndiri wokondwa kukhala ndi Mbale Borders muno, ndi atumiki ambiri ndi abwenzi.

<sup>5</sup> Mu sabata imeneyi ndi - ndinali kuganiza, ndi kuti “Ndikafika kumeneko Lamulungu ndikazindikira mtumiki aliyense, munthu ali yense.” Koma pamene wafika pano, umangotengeka mu uthenga mpaka umangiowala pafupifupi zonse, kotero - zinali zotero.

<sup>6</sup> Tsono, ndiyenera kubwerera ku Arizona. Ndiyenera kupita Lolemba likudzali sabata imodzi, kubwerera ku Tucson kukawasiya ana ku sukulu. Ndipo ndidzabwera pambuyo pake. Ndipo mkazi wanga ayenera kufika kumeneko mofulumira kukayamba - kukalembetsa anawo patatsala masabata awiri kuti sukulu iyambike. Ndipo ine . . . Kotero ndidzabworeranso kuno kwa kanthawi.

<sup>7</sup> Ndipo tsono, ino ndi nthawi yanga yopumula. Monga mukudziwa ndalalikira kuyambira mu December, January, February, March, April, May, June, ndiponso July. Tsono, ngati Mulungu afuna, osati kuitana kwa padera, ino ndi nyengo imene ndi - ndi - ndimapumula, nthawi yanga yopumula; ndimapita kukasaka. Ndipo ndi . . .

<sup>8</sup> Tsono, ngati Ambuye angandiitanire ku china chakenso, zinthu zimenezo siziri kunja kunja kwa chithunzi. Mulungu ndi woyamba nthawi zonse, ndipo ine ndikufuna Iye akhale woyamba. Koma ngati sipakhala kuitana kwina kwake ndi kumeneko ndiko kufuna kwake, chimenecho ndi chimene ndingachite tsopano kwa miyezi iwiri ikudzayo, ndikupita kukasaka. Tsono - kudzipumitsa. Ndi . . .

<sup>9</sup> Simukuzindikira, dziko lapansi silingadziwe chimene ndingapyole nacho. Mukuona? Ndipo ndi - changokhala choposyinja. Zosadabwitsa Ambuye anawauza ophunzira Ake pamene Anali kuyenda nawo, “bwerani panokha mu chipululu, pumulani mwa kanthawi.” Mukuona? Ndimazindikira chimenecho kwambiri tsiku lililonse, makamaka pamene masiku anga akuchulukirabe pa dziko. Mukuona? Pamene munthu ukukula umachizindikira ichi. Mukumva abusa athu akunenanso “amen” ku chimenecho. Iwo - tikhoza kuzindikira kuti sitiri anyamata pamene tapyola zaka makumi asanu. Tsono, . . . Tiyenera kukhala ndi kanthawi.

<sup>10</sup> Tiri othokoza chifukwa cha maumboni amene tangowamva kumene. Mkazi wanga anali kwa akazi a Wood dzulo pamene anthu ena anafika kuchokera ku Alabama, kwina kwake kumeneko, ndipo anali kufotokoza za zinthu zazikuru zimene Ambuye anachita mu msonkhano umenewo, ana aang’ono akumachiritsidwa ndi zinthu zina zosiyanasiyana, ndi zinthu zina zambiri kotero kuti . . . Mai, zingangotitengera nthawi yaitali ku - kuti tikitikoze.

<sup>11</sup> Kotero inenso ndiyenera kukumbukira kuti... Ndikhulupirira ena a iwo anandifotokozera kuti Mlongo Larson wakhala ali pano masiku awiri a Lamulungu ndi mwana wamng'ono. Sindikanadziwa, koma ndikukhulupirira ananena kuti anali muzukulu wao, mwinamwake kudzaperekedwa kwa Ambuye. Akuchokera naye ku Chicago. Mayiyo wakhala wachifundo kwambiri kwa ife, ndipo tiri - kumuyamikira iye. Ndipo anadza naye mwana wamng'ono kuchokera ku Chicago kuzaperekedwa, chimene wangokhala ndi nthawi yochepea kuti achiturutse, ndiganiza, kuti aperekedwe; koma ali wokondweretsedwa kuti mwana ameneyu aperekedwa kwa Ambuye. Kotero ngati Mlongo Larson pamene ndi kulankhula, akhoza kubwera naye mwana ameneyo kuzaperekedwa...

<sup>12</sup> Ndipo kotero mwina pamene akukonzeka, ndindikufuna kunena ichi kuti uthengawu wakhala wovutitsitsa mwa mauthenga onse amene ndakhala ndikuyesa kukonzekera mpaka usiku wathawu. Mu sabata lonseli ndakhala ndikupita mu chipinda, kuyesa kukhala pambuyo pa kuitanidwa kwanga ndi zina, ku - kuyesa kupeza china chake m'maganizo mwanga cha nthawi ino. Ndipo pamene ndipita, si-sindikanakhoza ngakhale...M'mutu mwanga munalibe chiri chonse. Kenaka dzulo ndinapita ku chipinda cha pansi. Ndinaganiza kuti kunatentha kwambiri kotero ndinapita ku chipinda chapansichi ndi kukhala pansi m'menemo. Ndipo ndinayesa kutenga Baibulo langa kuti ndiwerenge, ndipo ndinali kugona. Kotero ndimadzuka ndikumwa madzi, ndikuyesa kugiwedeza ndi kupita panja, ndi kuyendayenda, ndi kukhala pa sitepe.

<sup>13</sup> Winawake anadza nandiwona nditavula malaya, nditakhala pa sitepe; kunatentha kwambiri. Anandigwedezera mkono. Sindinadziwe ngati anandigwedezera mkono...Winawake, ayenera kukhala wing wake wa mu mzinda momwemuno, kapena ayenera kukhala winawake mu mpingo muno, anandigwedezera mkono. Ndipo ndi - ndinali ndikuganiza ndindinangoona mwamwayi pamene galimoto inali kudutsa. Ndinamgwedzera mkono.

<sup>14</sup> Usiku wapita ndinalowa mugalimoto ndi kukayenda cha ku Charlestown, kuyetsa kupeza china chake. Ambuye, anaoneka ngati, amafuna kundiuzwa china chake, koma ndi - Satana anali kuyesetsa kuima patsogolo panga kuti ine ndisachite chimenecho. Kotero ndinaganiza, "Chabwino, ngati achita chimenecho, ndingochedwerabe, kungoyem-bekezerabe, kumangomenya chitseko mpaka Atatsegula. Kotero kuti mu mphindi zowerengeka zapitazo, kapena itangopitirira 7 koloko m'mawa uno... Ndinadzuka m'mawa kwambiri.

<sup>15</sup> Dzulo, wodwala pang'ono, kuyetsa... Ndinadya chimanga china chimene sindinagwirizane nacho bwino, chikutentha kwambiri, ndipo ndi - ndinayesa kuchoka ku chimenecho. Ndipo - kotero kuti m'mawa uno cha m'ma 8 koloko,

ndinangotola Lembo limene linandizizwitsa ine. Ndipo ndinayang'ana Lembo limenelo kawiri, ndi kawirinso linandizizwitsa. Ndipo ndinalitsata m'Malembo; ndipo ndangotsiriza kumene maminiti owerengeka apitawo. Kotero kuyenera kuti Ambuye ali ndi uthenga kwa ife m'mawa uno umene Satana anayesa kuuletsa kuti usadze kwa ife. Mungabwere naye pano wamng'onoyo, Mlongo Larson? (Mbale Branham amupereka kwa Ambuye mwanayo - Mkonzi.) Mulungu akhale nawo ndi kuwathandiza.

<sup>16</sup> Tsono, ndakhala ndikukusungani Lamlungu litatha, masiku awiri, ndipo ndikuganiza - kapena misonkhano iwiri, m'mawa ndi madzulo, ndipo chimenecho chinali chovuta pa inu. Ndikumvetsa kuti ena a inu mumayenda mtunda wautali, ndikuphonya ntchito ya tsiku limodzi, ndi zina zoterozo. Kotero ngakhale tingaleke Lamlungu - Lolemba, sabata limodzi ndingolengeza msonkhano wa Lamlungu likudzali, Ambuye akafuna. (Mukuona?), pokhapokha ngati gulu lingafune kudzakhala - kusalirabe mpaka usiku. Mukuona? Ziri - ziri kwa... Alipo ambiri a inu. Ndi angati angafune usiku uno, tiyeni tiwone - tikhale ndi msonkhano usiku uno? Tsono, amene angafune kukhala nao Lamlungu likudzali, kwezani dzanja lanu. Wina... O mai, ndi woyandikira, mukuti chiani? Tsono, Ben...

<sup>17</sup> Ndinali... Uthengawu ndi wautali m'mawa uno, koma si-sindikudziwa m'mene... Ndipo ndikudziwa ndinathandizira kupanga malamulo a mpingo, koma m'menemo ngati mungaonetsetse ndinati, "pokhapokha ngati ndikujambula matepi." Mukuona, kotero uku ndi kujambula patepi. Kotero mwinamwake tidzayesa kubweranso nthawi zonsezi usiku uno, ndi Lamlungu limene likudzali, tidzali, tidza - ngati Ambuye angafune.

<sup>18</sup> Tsono, ngati simukhala ndi uthenga sabata lino, kotero mudzabwere Lamlungu likudzali. Ndimadana ndikuti inu muzibwera kawiri chomwecho, koma ndikuona tiri ndi kanthawi kochepa. Ndipo tangokumbukirani, ngati nthawi ikupita, sitikhalanso ndi mwayi umenewu kwa nthawi yaitali. Mukuona? Kumbukirani, chinachake chichitika. Mwina lamulo lidzatiletsa kapena Satana adzalowa pakati panu ndikukubalalitsani. Zakhala zikukhala moteromo. Mukuona? Chinachake chidzachitika. Kotero tiyeni tiyamikire miniti iliyonse imene tikukhalira pamodzi.

<sup>19</sup> Kotero tsono, kwa inu amene mungapite ku nyumba kwanu, usiku uno, udzakhala ngati usiku wa Lamlungu lapitali. Ndinangokhala ndi - ndi uthenga pang'ono waufupi. Kotero inu - ngati mukuufuna pa tepi, bwanji, tikutsimikiza tidzakutumizira tepiyo ngati mukubwerera kunyumba. Ngati si choncho, ndilalikira usiku uno ngati Ambuye afuna.

<sup>20</sup> Ndinali ndi zolemba zinazake dzulo kapena - kapena dzana, ka uthenga kochepe ndinangokalemba kuchokera mu kukumbukira kapena china chake, ndipo - ndi wa nthawi yaitali. Ndi mauthenga awiri a - ngati umodzi mwa iwo ndi 'Chitsime Chong'aluka,' kapena, 'Kufetsera ku Mphepo ndi Kututa Kamvuluvulu,' ndi uthenga wabwino. M'mawa uno ndikuphunzitsa. Koteronso usiku uno ndilankhula za 'Kufetsera ku Mphepo ndi Kututa Kamvuluvulu,' kapena mwina, 'Chitsime Chomwe chiri Kuchucha.'

<sup>21</sup> Kotero m'mawa uno ndikufuna kuwerenga kuchokera m'Malemo oyera tsopano. Kodi mwakhala motakasuka? Nenani, "Amen." (Gulu libvomera "Amen!" - mkonzi.) Ndi zabwino zimenezo. Tsono, ndikufuna inu mutsegule m'MaBaibulo anu pamodzi ndi ine ku Bukhu la Hoseya, inu amene mukukhumba kuwerenga. Ndipo tiyeni tiwerenge ma Vesi owerengeka kuchokera pa chaputala 6 cha Bukhu la m'neneri Hoseya. Tiyeni tiimirire.

<sup>22</sup> Mulungu wokonedwa, sitiri oyenera kutenga Bukhu ili m'manja mwathu, pakuti timawerenga m'Malemo kuti panalibe munthu aliyense m'mwamba kapena pa dziko lapansi kapena pansu pa dziko la pansu amene anali oyenera ngakhale kukhoza kutenga Bukhulo kapena kuyang'anamo. O, ndipo anadza. M'modzi amene ana - monga mwana wa nkhosa wophedwa; Anatenga Bukhulo chifukwa Anali woyenera; kotero anamusula zisindikizo. Ndipo tikuyang'ana kwa Iye m'mawa uno kuulula thandauzo la chimene chalembedwa m'Bukhu ili, chifukwa ndi Bukhu la chiombolo; onse amene awomboledwa alembedwa m'menemo. Tingopeza malo athu m'mawa uno mu nthawi imene ife tikukhalamo. Pakuti tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

*Tiyeni, tibwerere kunka kwa YEHOVA; pakuti wang'amba, nadzatipoletsera; wakantha, nadzati manga.*

*Atapita masiku awiri adzatitsitsimutsa, tsiku lachitatu adzatiutsa; ndipo tidzakhala ndi moyo pamaso pake.*

*Tidziwe tsono, tilondole kudziwa YEHOVA: kuturuka kwake kwakonzekeratu ngati matanda kucha; ndipo adzatisera ngati mvula, ngati mvula yamasika yakuthairira dziko.*

*O Efraimu, ndidzakuchitira chiani? O Yuda, ndikuchitira chiani? Pakuti kukoma mtima kwako kukunga mtambo wa m'mawa, ndi ngati mame a mmawa aphwa.*

*Chifukwa chache ndawalikha ndi aneneri; ndawapha ndi Mawu a pakamwa panga; ndi maweruzo anga aturuka ngati kuunika.*

*Pakuti ndikondwera nacho chifundo si nsembe ai; ndi kumdziwa Mulungu koposa nsembe yopsereza.*

*Koma iwo analakwira chipangano ngati munthu, m'mene anandichitira monyenga.*

*Gileadi ndiwo mzinda wochita kusaweruzika ndipo waipitsidwa ndi mwazi.*

*Ndipo ngati magulu a mbala alindira munthu, momwemo msonkhano wa ansembe, amapha pa njira yakugwirizana; nachita choipitsitsa.*

*Ndaona chinthu choopsetsa m'nyumba ya Israeli. Pamenepo pali chiwewere cha Efraimu, Israeli wadetsedwa.*

*Wakuikiranso nyengo yakukolola, O Yuda, pamene ndikabwezanso undende wa anthu anga.*

<sup>23</sup> Ambuye Yesu, tengani ulamuliro kuchokera apa ndi Mzimu Wanu Woyera mutu umene wafunika pamene tikudikirabe pa Inu. Mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>24</sup> Tsono, mutu wa nkhani yanga m'mawa uno ndi; "Kuzindikira Tsiku Lanu Ndi Uthenga Wake." Tikuona kuchokera mu phunziro la Lamlungu wapitawo, pamene tinaphunzitsa Phwando La Malipenga. (MAWU OLANKHULIDWA, VOL. 3 NO. 6 - mkonzi)...Ndipo ndikufuna mumvetse tsopano nthawi imene - nthawi ya a Israeli mu wotchi ya Mulungu.

<sup>25</sup> Lero tikuchita ndi phunziro la Sande Sukulu limene ine ndikufuna kuti mudziwe. Ndi kuzindikira nthawi imene tikukhalamo. Tangotsala pang'ono kutha monga mukuona, Tsono ndi ichi muyenera kudziwa ora lenilenilo, ndi nthawi ndi chizindikiro, ndi uthenga umene mungaulandire.

<sup>26</sup> Tsono, monga tinayambira Lamlungu lapita..Takhala tikulankhula za kukalalikira Malipenga, Malipenga Asanu ndi Awiri otsiriza mu Baibulo. Ndipo ine mwa ine ndekha, ndimaganza kuti adzatuluke chimodzimodzi ngati mu zisindikizo. Koma ndawonetsetsa kuti pa kutsegula kwa chiri chonse pakhala chinthu chachikuru chikuchitika. Monga tinalalikira mibadwo Isanu ndi Iwiri ya Mipingo...ndipo inalali yangwiro, mpaka Mzimu Woyera Mwiniwake anatsikira pakati pathu ndi kubvomereza, ndi kuchiika mu nyuzi ndikufalitsa ku mtundu wonse, ndipo kuchiwonetsa pa mwezi m'mwamba, ndikuchitsimikizira kwa ife patatsala masabata ndi miyezi chisanachitike kuti - mwa njira imene zidzakhallira mwangwiro. Muno mu chihema Anachizindi-kiritisa. Pano pa - mu nthawi imene Anachizindikiritisa pa mwezi ndi pa dzuwa; anachizindikiritisa. Ndipo momwe maiko aimira nthawi ino, Anachizindikiritisa pamene papa wa ku Roma anachoka napita

ku Palestina; anali papa woyamba chiyambire (amatsimikizira kuti) Petro, anali papa. Tsono, zinali zochititsa mantha.

27 Kotero tikuona zisanadze zisindikizo zisanu ndi ziwiri zimene zinabisa zinsinsi zonse...Ine osazindikira zimene ndinali kujambula pa bolodi za mibado ya mpingo, sindina... Mulungu akudziwa. Mwa masopenya ndinajambula, ... Osazindikira kuti pakatha chaka ndi miyezi isanu ndi umodzi, Mulungu adzachitsimikizira m'mlengalenga ndi mwezi ndi kuchiika pa nyuzipepa ya dziko lino. Sindinadziwe chimenecho. Osadziwa kuti padzakhala mdima wozizwitsa pa mwezi kuyimirira m'badwo uno wa Laodikaya.

28 Tsono, pa mapepala mungopezapo mibadwo isanu ndi umodzi yokha. Ndi chifukwa chakuti mpingo wa Laodikaya unali mdima wokhawokha. Ndipo mungaonetsetsa chimene chiimirira iwo mu mzimu monga m'mene Mulungu anachilankhulira mwamba...Pamene ndinachijambula pansi pano, ndimasiya kampata pang'ono penipeni, monga mukuona, kuwala kwa pang'ono zedi; inali isanakwanitsitse nthawi yakuitana osankhidwawo kuchoka m'dziko, ndi chifukwa chake ndinaika mu m'badwo wa chisanu ndi chiwiri; koma pamene Mulungu anachilemba m'mwamba, panali mdima wokhawokha. Zikuthandauza kuti mwina wotsiriza waitanidwa kale mu m'badwo wa Laodikaya umemewo; sitikudziwa. Payenera kukhala ulaliki pa chimenechi.

29 Tsono, onetsetsaninso zisanadze zi-zisindikizo zisanu ndi ziwiri, zimene sindinakhale nalo ganizo loti zikhala moteromo...Pano pa chihema Anachilankhula nanditumiza ku Tucson, Arizona, kukufotokozerani zonse zimene zingadzachitike. Kotero pali munthu amene ali pano lero amene anali kumeneko kuona zikuchitika momwemo m'mene anafotokozerana pano kuti zidzachitika, Anadza angelo asanu ndi awiri. Kotero a nyuzipepala ndi a magazini, anachilemba m'dziko monse muno: Kuwala kozizwitsa m'maonekedwe a chi piramidi, monga m'mene ndinajambulira pano ndi kukuonetsani kunachokera pamene angelowo anaime ndi kukwera m'mwamba mwa maiko makumi atatu ndi ma mailo makumi awiri ndi mphamu zisanu ndi ziwiri kutambalala kwake, kapena kuti kukwera m'mwamba ndi mamailo makhumi awiri ndi mphamu zisanu ndi ziwiri ndi kutambalala kwake ma mailo makumi atatu, ndaiwala kuti zinali ziti. Ndipo zinaoneka mdziko monse muno, uko ku Tucson, Arizona, ndi kumene zinachitikira, nthawi yomweyo.

30 Mukuona - Baibulo... Mulungu siwo... Ichi si choti munthu wina akungoyesa kukukanikizirani chinachake kwa inu, koma kukuululirani za uzimu za nthawi ino.

31 Tsono kotero, uthenga wotsatira...umene unatsegula Zisindikizo Zisanu ndi Ziwiri, zimene zinamasula zinsinsi

zobisika zonse za mu Baibulo, ziphunzitsa ndi zina zotero, zimene dziko limatsutsana nazo mwamwano masiku ano, kuti ndi zolakwika izi, kuti . . .

<sup>32</sup> Tsiku lina kuno ku Arizona, anatenga ndi kusokoneza ma tepi kuyesa kundipangitsa ine kunena zinthu zimene sindinazilankhule. Mungokumbukira masomphenya a zolingalira za ku Arizona. Baibulo linanena kuti kunali kwabwino kwa inu kuti mukanaikidwa mphero pa khosi panu. Ndipo chinthu china: “kuti wina aliyense amene (khaya ndi wolalikira kapena ndi ndani) akachotsapo liwu limodzi kapena kuonjezapo liwu limodzi. . .” Anthu kuika matanthauzo awo awo pa Mawu pamene Aperekedwa, kuyesa kuwupangitsa kuti anene china chake chimene ine sindinachilankhule, ndipo osati Mawu anga, ndi Mawu Ake. “Nandi amene angaonjeze kapena kuchotsera. . .”

<sup>33</sup> Kotero m’masomphenya taona aneneri awa akutsika, monga m’mene ndinafotokozera kwa inu, ndikhulupirira, masabata angapo apitawo. Zonse zidzakhala choncho. Ndinati, “muzingoyembekezera.” Pamene ine ndikhala ndikumenya, Mulungu sangamenye. Koma tiyeni timuleke Iye achite. Ndi Iye amene amatisamalira. Mukuona?

<sup>34</sup> Tsono, tinaonetsetsa Lamlungu lapitali kunali - kulalikira masiku a phwando. . . la Pentekositi. Ndipo pakati pa Phwando la Pentekositi ndi Phwando la Malipenga panali nyengo yaitali, masiku makumi asanu pakati pa Pentekositi ndi Phwando la Malipenga. Ndipo masiku makumi asanu, chimene Pentekosti amathandauza “Makhumi asanu”; ndipo kunali kuweyula - mitolo, kapena kusunghanitsa, zipatso zoyamba kukololedwa zinali kubweretsedwa. Ndipo tikuona kuti ndi zipatso zoyamba za chilengedwezi zinali mthunzi, kuimirira zipatso zoyamba za Mzimu Woyera zimene zidzaweyuliridwa pa anthu. Ndipo tikuona kotero kuti masiku makumi asanu amenewo analandiridwa ndi Amitundu, amene Mulungu anawaitana kuchokera kwa Amitundu, anthu a Dzina Lake - Phwando la Pentekositi. Kotero takhala tikupitirirabe mu Phwando lalitali limenelo la Pentekositi.

<sup>35</sup> Tsono, kwenikweni pa masiku makumi asanu amenewa pakhala masabata asanu ndi a awiri enieni. Ndipo masabata asanu ndi awiri anaimirira Mibado Isanu ndi Iwiri ya Mipingo yodzaitanidwa mu nthawi ya Pentekositiyi - Phwando la Pentekositi, kuitana anthu chifukwa cha Dzina Lake kuchokera kwa Amitundu. Tsono kumapeto kwa masabata asanu ndi awiri amenewa amene akhalapo kale, kukanakhala Tsiku La Chitetezero, limene linali la Malipenga Asanu ndi Awiri. Ndipo Malipenga Asanu ndi Awiriwa anali oitanira tsiku la kusisima kubwerera ku nsembe kapena Chotetezera. Kotero tikuona kuti Israeli; Malipenga Asanu ndi Awiriwa anali a Israeli okha.



<sup>36</sup> Tsono kotero, chifukwa chimene sanandilole ine kuti ndilalikire Malipenga Asanu ndi Awiriwa... Ngakhale ine ndinali wokonzekera kulengeza, maholo anakonzedwa ndi zina zonse kuti ndipite ndikalalikire Malipenga Asanu ndi Awiri. Ndipo ndinati, "Pali china chake chimene chikundivuta kwambiri." Ndinati... Tinapitirizabe kugwira ntchito, ndipo Billy ndi ena tonsefe, kuyetsetsa kuti zonse zikonzeke za nyumba ya mpweya wabwino ya pa sabata limene likudzali la Malipenga Asanu ndi Awiri, pokhala ndi masiku khumi - kapena masiku asanu ndi awiri. Tinali ndi nyumba yochitiramo msonkhano ya sukulu. Koma Mzimu Woyera sanandilole kuchita pa chifukwa china. Kotero ndinadabwa chifukwa chiani. Ndipo pamene ndinalowa kukapemphera... Ndinamuza mkazi wanga, "Ndikulowa." Ndipo moona mtima ndinagwada pansi pamaso pa Mulungu kupemphera. Kotero Anandibvumbulutsira Malipenga Asanu ndi Awiriwo kuti analira mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi, ndipo ndinawalalikira mwa uzimu. Mukuona? Ndi dzanja la Mulungu, zonse. Ndi za a Israeli; ndipo tinazinena mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi, inu amene muli ndi tepiyo, m'mene mazunzo a Ayuda...

<sup>37</sup> Nthawi ya Amitundu inali mu phwando la Pentekositi. Malipenga, onse analira mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi. Ndipo tinawatenga Lamulungu lapitali mu Phwando la Malipenga, ngati inu nonse mukufuna kumvera. (MAWU OLANKHULIDWA, Vol.3 No.16 - Mkonzi.) Akanachita chiani? Kufulumizitsa Ayuda kuchokera ku mbali zonse za dziko kupita kwao. Chiyenera kukhala pamenepo. Ndi kumasula kwa Zisindikizo mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi, ndi mu... Malipenga Asanu ndi Awiri analira mu-mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi.

<sup>38</sup> Tsono, Uthenga wa mngelo wa chisanu ndi chiwiri ndi womasula zinsinsi za Zisindikizo, kuitana antchito a Amitundu pa ora la khumi ndi kulandira malipiro ofanana ndi amene analandira antchito a ora loyamba. Mukuona? Tsono, Yesu anachiphunzitsa. Anati panali anthu ena amene anapita kukakolola. Anali a ganyu, ndipo pamene anagwira - m'mawa analandira n - n - nthawi, kobidi la tsiku limenelo. Ndipo dzuwa liri pa liwombo wina anadza nagwira ntchito. Ndipo kotero pa ora la khumi ndi limodzi, limene liri ora lotsiriza la tsiku, winayonso anadza nalandira malipiro ofanana ndi amene analandira wa pa ora loyamba la tsikulo, ora lomaliza.

<sup>39</sup> Ndi za ngwiro, m'mene amithenga a ora loyamba ndi Mawu, ndi Uthenga, ndi Choonadi anadza pa tsiku la Pentekositi. Ndipo kunali mbado wa mdima umene unawatsekereza. Kotero pakati pa tsiku, Luther, ndi Wesley, ndi ena anadza. Tsono kotero kuyenera kukhala Uthenga wa nthawi ya madzulo, ndipo kulandira chinthu chomwecho anachilandira poyamba. Uthenga

wa madzulo ndi wobwezeretsanso, kubwezeretsanso chinthu chomwecho kawiri.

<sup>40</sup> Ndipo kumbukirani masomphenya a sabata yatha, kuti pamene Mkwatibwi anadza kudza - kuonetseratu. Anadza Mkwatibwi wochepa wokongola, mu masophenya. Ndipo ndiri osaganizira za icho, kungokhala pamenepo kumayang'anira kunja. Ndipo apo anadza Mkwatibwi. Ndinamva Liwu pambali panga, linati, "Uku ndi kuonetseratu kwa Mkwatibwi." Ndipo anadza pafupi. Ndinamuonetsetsa Iye, m'mene anakhallira, wooneka mokongola kwambiri, wokongola, wa msinkhu wochepa. Anali kungoyenda sitepe imene angaithe osati moguba, koma m'mayendedwe a - a mzimai, m'mene anali kuyendera mwa chisomo, ngati mkazi. Ndi m'mene anali kuyendera, akudza cha kumanzere kwangaku mbali iyi. Ndipo anapita osampenyanso.

<sup>41</sup> Ndipo Ananditembenzira mbali ya kumanja, ndipo anandionetsa mpingo uli wonse monga m'mene unachokera mu mibado yonse. Ndipo O, zoipa bwanji! Ndipo wotsiriza wake unali mbado wa mpingo wamasiku otsiriza ano; umene unasogozedwa ndi mfiti. Ndipo anali obvala mosayenera, onyansa m'maonekedwe, Ndipo anali kuguba mwa njira ya gwedemula ndi sinjonjo. Ndi azimai amenewo akuziponya mwa gwedemula, atangodziphimba ndi pepala lotumbululuka, mokhumbiritsa. Liwu...kutumbuluka ndi maonekedwe a pakati pa choyera ndi chakuda, umene uli mtundu wonyenga. Chotumbululuka si choyera kapena chakuda Ndi mtundu wonyenga. Ndipo pepala looneka ngati la mbu atagwiriza patsogolo pao, ndi masiketi ong'amba m'mbali atagwiriza patsogolo pao; ndipo anali amariseche enieni kuchokera m'chiuno mwao kupita m'mwamba. Ndipo anali kuguba ku - kapena nthawi, kapena kugwedemuka ndi kumapitiriza ndi nyimbo imeneyo, akuyenda. Ndipo ndinati "Umenewo ndiye Mpingowo!"

<sup>42</sup> Ndipo pamene unandipyola, mtima wanga ngati ukomoke. Ndinaganiza, "Ngati umenewo uli woti ukaperekedwe kwa Khristu ngati mkwatibwi... Mwa mphamvu yonse ndi zinthu zomwe anthu achita kuyesa kubweretsa mkwatibwi wa Khristu - ndipo wonyansa, woipa, wooneka - wonyansa, hule ngati ameneyo akhale mkwatibwi wa Khristu?" Zinandidwalitsa mu mtima mwanga!

<sup>43</sup> Ndipo pamene anali kudutsa, atatha iye...Asanafike pamene tinaima, anali kugwiriza pepala patsogolo pake, akugwedemuka ndi kudumphadumphaka akuzithyolera mbali iyi ndi mbali ina akupita, ngati ma vinidwe a makhono amene ali nawo a masiku ano, akudzigwiritsa ntchito yekha mu njira yosayenera pamene anali kuyenda.

44 Ine sindikayankhapo pa zinthu zimenezi. Ndingolankhula zimene ndaziwona! Ndipo Mulungu ndi Woweruza wanga. Koma umenewo unali mpingo wochokera ku U.S.A. (kwa Amerika).

45 Tsono, pamene anali kudutsa, kumbuyo konse kunalibe chophimba ai. Ndipo kotero pamene anali kudutsa ndinamva kukomoka ndi kudwala.

46 Kotero Anati, “Mkwatibwi abweranso mu kuonetseratu kwachiwiri,” Ndipo apa Mkwatibwi anadza pambuyo pake, wooneka momwemo ngati Mkwatibwi amene anadutsa poyamba paja. Kotero mtima wanga unadumpha ndi chimwenwe podziwa kuti kudzakhala Mkwatibwi. Ndipo adzapangidwa kuchokera ku chinthu chomwecho nadzavala chovala chomwecho ngati woyambayo. Adzaitanidwa. Ndipo ndikudziwa kuti ndi Choonadi. Ngati chimenechi si Choonadi, kotero masomphenya ali onse amene ndakhala nao mbuyomu anali olakwika. Ndipo aliyense akudziwa kuti chiri chonse chimene Wakhala akutiua chinali Choonadi. Chinangokwaniritsidwa monga. . .

47 Kotero mukuona kunyansa kwa mpingo wamakono, wozitcha wokha mpingo?

48 Monga wina ananenapo tsiku lina, Mbale Ruddell, mbale wanga wofunika kwambiri amene waima mosamira khoma apoyo tsopano, kuti anauwona ngati mphukira pa mpesa. Ndipo tinali kukambirana m’chipinda tsiku lina. Ndipo Mbale Ruddell anatokonezedwa ndi m’mene nthawi yakhalira ndi - ndi m’mene mzimu ukudzera mu mipingo lero, m’mene ukuyambira kutsika. Atumiki akudza kuchokera mbali zonse, akufunsa za ntchito pano, “Chachitika ndi chiani, Mbale Branham, chachitika ndi chiani?” O mai!

49 Mbale Ruddell anandifunsapo funso, “Kodi moyo wao amautengera kuchokera kwa Satana, kapena chiani.”

50 Ndinati, “Ai, mpesa womezanitsidwa umakhala moyo kuchokera pa mpesa weniweni.” Umakhala moyo, chifukwa chipatso chonga malalanje. . . Ndimu lidzakula pa mtengo wa malalanje koma silidzabala malalanje, ngakhale ukukhala m’moyo wake. Ndipo mpingo wongotchulidwa, wangokhala womezanitsidwa kukhala pansu pa dzina la chipembezo mu dzina la Katolika ndi Protestanti, wongomezanitsidwa kumadya kuchokera ku Mpesa weniweni, komabe kubala zipatso zomwe iwo ali, chifukwa sanatembenuke. Sanali mu chilinganizo cha kudziwiratu cha Mulungu. Ndi chifukwa chake ayenera kukana Mawu ndi kubala zipatso za mtundu wina. Mtengo weniweni ndi mizu yake unadziwidwiratu kuti ubale malalanje pa mtengo wa malalanje. Yesu anati, “Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi.”

51 Koma ngati mtengo umenewo utulutsanso nthambi ina, idzabala zipatso zake zenizeni. Ndipo kuyenera kukhala kubwezeretsanso kwa zinthu zonsezi kumapeto kwenikweni kwa Mpesa. Kuyenera kukhala - kudze kubwezeretsa,



<sup>56</sup> Tsono, mwamuna akudza, ndipo mkazi amatenga dzina lamwamuna. Amitundu akhungu amene sakuliona Dzialo, Ambuye Yesu Khristu, mu ubatizo. Ndi zoipa kwambiri, koma ziyenera kukhala momwemo. Ayuda, anayenera ku - anayenera kusaona chimenecho. Pali m'modzi yekha amene angaone chimenechi; ndi amene anasankhidwiratu kuti achione. Apo ai simudzachiona chimenechi. Ayuda sangaone kuti anali Mesiya wao, koma chikhalirecho anali ophunzira ndi ophunzira Malembo, anthu a maphunziro odziwika, amawerenga Baibulo limene inu mukuwerenga. Tsono, pamene chadziwitsidwa kwa ife, tikuona poyera kuti anali Mesiya. Koma sanakhoze kuchiona. Sangachionenso ngakhale lero. Aneneredwa kuti ali akhungunso.

<sup>57</sup> Mpingo lero waneneredwa kuti uli wakhungu, kuukana Uthenga wa nthawi ya madzulo; Chibvumbulutso 3 anatero: "Ndiwe watsoka, womvetsa chifundo..." Onetsetsani m'mene Mkwatibwi anakhalira usiku wina - kapena mpingo; wamariseche, wakhungu, ndipo sukudziwa! Ambuye, Yesu mutichitire chifundo! Baibulo linati anali wamaliseche. Ndinali ndisanawone mpaka tsopano lomwelino. Mpingo we Laodikaya unali wamariseche. Ndipo pamene unaonekera usiku wina, unali wamariseche (osachizindikira), ndipo sakudziwa!

<sup>58</sup> O, tikuthokoza zedi, m'mene... Mosadabwitsa tikuyamika kwambiri. Ndikuona ngati sitikuyamika mokwanira pa zinthu zimene Mulungu akutizindikiritsa.

<sup>59</sup> Wamariseche! Ndipo masomphenya anati-anandionetsa kuti unali wamariseche koma sunadziwe. Achititsidwa khungu ngati m'mene Israeli anachititsiridwa khungu, kotero kuti Amitundu akhoza kulowa, tsono Amitundu achititsidwa khungu kutero kuti Mkwatibwi akhoze kutengedwa ndipo Israeli akhoze kulandira Phwando la Malipenga. Zangokhala za ngwiro.

<sup>60</sup> "Atapita masiku awiri adzatitsitsimutsa (kapena kutipatsa chitsitsimutso), kutisonkhanitsa pamodzi (Ayuda akulankhula za Malipengawa tsopano). Ndipo Adza - ndipo tidzakhala amoyo Pamaso Pake (kapena kukhala ndi Moyo Wosatha. Mukuona?) Tidzakhala pamaso pake." Baibulo linati apa pa Hoseya, "Ndipo tidzakhala pamaso Pake (Umenewo ndi Moyo wa Iye Mwini, Moyo Wosatha), kukhala ndi Moyo pamaso Pake." Iye wakutsata zomkondweretsa adafa ngakhale ali ndi moyo. Kotero tikulonjeza kuti Israeli adzakhalanso ndi Moyo pamaso Pake. Wakhala wakufa ku zenizeni ndi ku phwando la Pentikositi.

<sup>61</sup> Tsono onetsetsani mosamala. Kotero patapita masiku awiri... Tsono, chimenechi sichikutanthauza masiku awiri a ma ora makhumi awiri ndi mphambu zinai, chifukwa zakhala - chimenecho chinachitika m'mbuyomu zaka mazana apitawo. Chimathandauza masiku awiri ndi Ambuye - patapita zaka zikwi ziwiri. Tsono, mukudziwa kuti papita zaka zingati

kuyambira nthawi imeneyo? Papita zaka mazana makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi ziwiri kuyambira nthawi imeneyo, chifukwa pa Hoseya apa ndi B.C. 780-1964. Mukuona, ndi china chake chopitirira zaka 2700 zapitazo. Anati, “Patapita masiku, awiri, mu tsiku lachitatu, adzatitsitsimutsanso ndikutipatsa Moyo pamaso Pake.” Apo pakudza Malipenga anu. Iyi ndi nthawi imene tikukhalamo, tsiku limene tikukhalamo.

<sup>62</sup> Tsono, abalalitsidwa, achititsidwa khungu, asonkhanitsidwa ndipo alowa kwambiri mu tsiku lachitatu. Mukuchiona chimenechi? Anabalalitsidwa pa dziko lonse lapansi kuchoka ku Palestine. Anachititsidwa khungu kuti amukane Mesiya. Koma tsopano asonkhanitsidwa mu dziko mwao, kukonzekera Malipenga kuzindikira Chitetezero. Monga Baibulo linanena, akachilandira namupeza Iye ndi zipsera za misomali (Mpingo utatengedwa kale) ndipo adzanena, “Unazitenga kuti zipsera izi?” Iye anati, “Mnyumba ya okonedwa anga.” Ndipo Anati adzalekanitsa, banja liri lonse, ndipo adzalira ndi kunthunthumira kwa masiku, ngati banja limene linataya mwana wao yekhayo wa mwamuna. Ndipo kumbukirani Phwando la Malipenga lichita zimenezo - kunthunthumira, kuisima chifukwa cha Nsembe yophedwa; imene anaikana.

<sup>63</sup> Ali mu dziko mwao. Anabalalitsidwa, nachititsidwa khungu - ndipo tsopano asonkhanitsidwa. Ndipo zonse zinali mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi momwe Malipenga awo Asanu ndi Awiri analira kudzawason-khanitsa pamodzi. Malipenga Asanu ndi Limodzi. . . La chisanu ndi Chiwirilo ndi Lipenga lopambana lija (monga tinali nalo Lamlungu lapitali). Malipenga Asanu ndi Limodzi analira Mu Chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi, monga m'mene Chisindikizo chathu cha Chisanu ndi Chimodzi chinatsegulidwa, zonse nthawi yomweyo; awo okha onse analira kamodzi pamodzi, pamene ta takhala zaka zikwiri ziwiri mu phwando la Pentekositi.

<sup>64</sup> Tsono papita zaka 2700 kuyambira nthawi imeneyo. . . Anati, “Mu tsiku lachitatu tidzasonkhanitsidwanso. Papita masiku awiri, mu tsiku lachitatu tidzasonkhanitsidwanso ndikulandira Moyo pamaso Pake.” Mukuliona lonjezanolo? Ora linalembedwa mwangwiro pakhoma. Tikuona pamene tikukhalapo.

<sup>65</sup> Tsono mu dziko lakwao akuyembekezera Phwando la Malipenaga, kapena kuchizindikira chotetezeracho, ndi kuyembekezera kudza kwake, kudzalira chifukwa cha kuchikana kwao kumene anachikana nthawi yoyamba; ali ku dziko la kwao chifukwa cha chimenecho, kuyembekezera pamene iwo onse. . . Zonse zaikidwa m'malo mwake.

<sup>66</sup> Monga mtumiki wa Uthenga sindikuona chinthu chimodzi chotsala koma kupita kwa Mkwatibwi. Ndipo mkwatibwi ayenera kuchotsedwa iwo asanazindikire chimene

chinachitika. Anamangidwa, nabalalitsidwa - ndikuthandauza anabalalitsidwa, anachititsidwa khungu, ndipo tsopano asonkhanitsidwa. Chatsala ndi chiyani? Mkwatibwi achotsedwe, kuyembekezera kupita kwa Mkwatibwi wake, kotero aneneri awo a pa Chibvumbulutso 11 akhoza kuwaitanira ku Phwando la Malipenga, kuwapangitsa iwo azindikire chimene anachita.

<sup>67</sup> Kumbukirani, pakati penipeni pa zisindikizo zimenezo, chinadza chisindikizo cha Chisanu ndi Chimodzi, ndipo anali osankhidwa ndi oitanidwa 144,000. Ndipo pakati pa Lipenga Lachisanu ndi Chimodzi ndi Lachisanu ndi Chiwiri, Chivumbulutso 11 chionekera penipenipo mu m'ndandanda wa Chisindikizo Chachisanu ndi Chimodzi.

<sup>68</sup> Kuchita chiani? Kudzachita chiyani? Ichi chinali kudzabweretsa mboni ziwiri, Mose ndi Eliya, aneneri; chifukwa Ayuda amakhulupirira aneneri awo. Ndipo adzadza ndi chizindikiro cha aneneri, ndipo ntchito yao idzakhala ya mneneri, chifukwa anachita momwemo, kuonetsa chinthu chimodzi kuti munthu ukafa, kapena chinachake - pamene uchoka mu dziko muno chikhalidwe chako sichimasintha. Ngati uli wabodza tsopano, udzakhala wabodza kumeneko. Ngati uli woumamutu pano, udzakhala wouma mutu kumene ko. Ngati uli wokaika pano, udzakhala wokaika kumeneko.

<sup>69</sup> Amuna ndi akazi, ndi nthawi yoti mudzigwedeze nokha ndi kudziyesa nokha, ndikuona pamene tikuima! Chifukwa imfa simatisintha. Apita kwa zaka zikwi; Mose kwa zaka pafupifupi makumi awiri ndi mphambu zisanu, ndipo Eliya kwa - chiyambire - pafupifupi zaka mazana makumi awiri ndi mphambu zisanu chipitire Eliya ndiponso Mose. Kotero pano abwereranso ndi chikhalidwe chomwecho nachita chinthu chomwecho. Imfa sichita kanthu kwa munthu koma kungosintha malo ake okhalamo, simasintha chikhalidwe chanu, siyimasintha chikhulupiriro chanu, siyimasintha chirichonse mwa inu koma malo anu okhalamo.

<sup>70</sup> Kotero khaya chikhalidwe chanu chiri motani m'mawa uno... Ngati muli okaikira Mawu a Mulungu, mudzakhala okaikira kumeneko. Sindisamala khaya muli oyera motani, mukukhala motani, ndipo mumakhala abwino motani kufa sikudzakusinthani ndinpang'ono pomwe, malo anu okhalamo basi. Ndipo ngati simungalandire Mawu onse a Mulungu m'mene alembedwera, simungatero kumeneko; kotero musadandaule, simudzakhala kumeneko. Muyenera kuwalandira mu uphuphu wake, mu mphamvu ya kutsimikizira kwake ndi vumbulutso la chimene ali; kotero mumasandulika gawo la chimenecho. Ndi Mawu Ake okha amene adzawautse, monga m'mene Iye anachitira ndi Mawu Ake pa m'mawa wa chiukitsiro choyamba Mawu Ake okha anaturuka pamodzi ndi iwo amene anafa m'Mawu Ake, kukhulupirira Mawu Ake ndi kutsimikizira Mawu Ake.

<sup>71</sup> Onetsetsani. Tsono ndi zaka mazana awiri ndi mphambu zisanu ndi ziwiri zapitazo (2700). Onetsetsani anabalalitsidwa, nachititsidwa khunyu, koma tsopano asonkhanitsidwa. Tsono, chinthu chotsatira ndi chakuti alandire Moyo.

<sup>72</sup> Ndipo Amitundu aitanidwa. Mkwatibwi wakonzeka. Mkwatulo wayandikira. Kodi tingazindikire chimenecho? Kodi tingakhulupiriredi chimenecho? Kodi ndi nthano yongonedwa? Kodi ndi zongopeka kwa ife? Kodi ndi chinachake chomveka chenicheni? Kodi ndi chinachake choti ife tiri kunja tingakhulupirire? Kapena ndi chinachake chimene chiri mwa ife, chimene chiri gawo lathu, chimene chiri choposa moyo kwa ife? Kodi malingaliro athu amene tiri nao muchihema muno m'mawa uno ndi otani? Kumbukirani, kudzakhala kagulu kochepa kamene kamaulandira.

<sup>73</sup> Tsono mu dziko lakwao kudikirira Malipenga. Tsono kuyembekezera kupita kwa Mkwatibwi kotero kuti Chibvumbulutso 11 chikwaniritsidwe. Mbadwo wa mpingo wathu. Zisindikizo zamatsulidwa zimene zatsimikizira chimene anachisiya mu mibadwo ya mipingo. Ndipo uthenga waperekedwa. Israeli ali pamalo ake (Aleluya!), kukonzekera Phwando la Malipenga.

<sup>74</sup> O, anthu inu m'maiko ena kumene mudzamve tepi iyi, simungadzuke, mbale wanga? Kapena zikukuchititsani khungu? Mungautaye ndikunena kuti ndi uneneri wonyenga pamene watsimikiziridwa pamaso panu ndi dziko lapansi, ndi nthawi, ndi anthu, ndi Mzimu Woyera Amene anachilemba chimenechi. Zatsimikizirikwa ndi chilengedwe, mwa uzimu, ndi zosakhala mwa uzimu. Zonse zimene anazilankhula zakwaniritsidwa ndi kutsimikiziridwa.

<sup>75</sup> Israeli ali mu dziko mwake, anawapititsa kumeneko, kuwasonkhanitsa m'menemo ngati nkhoa. Mimbulu inawalondola ndikuwathamangitsira ku chitetezo ku dziko lakwao. Kumbukirani, Israeli analonjezedwa kudalitsidwa pokhapokha ali mu dziko mwake. Mulungu sanadalitsepo Israeli ali kunja kwa dziko lake. Abraham anatsulidwa ataturuka m'dzikomo. Aliyense amene aturuka mu dzikomo ndi wotsutsidwa. Mulungu angadalitse Israeli pokha pamene ali mu dziko mwake. Kotero ali kumeneko tsopano ngati mtundu. Ndipo Mpingo waitanidwa. Ukungoyembekezera kukwatulidwa kwa Mkwatibwi kuchotsedwa.

<sup>76</sup> Zisindikizo zamasulidwa. Zaululidwa kwa ife. Taona zimene anazisiya. Inu amene mukufuna kutsutsana ndi kubvutika ndi za mbeu ya chinjoka, ndi ubatizo wa madzi ndi zina zoterozo, mwachititsidwa khungu ndipo simukudziwa. Mulungu wa dziko lino wakuchititsani khungu ku icho ndipo simukudziwa. (Zosadabwitsa ndinakhala ndi nthawi imeneyo m'mawa uno kulimbana ndi mphamvu zimenezo).



77 Kotero a - aneneri awo akhoza kuululidwa mu tsiku lotsiriza ili. Sangachite kupyola mu malipenga a - mpaka mu Phwando la Malipenga.

78 Ananena mwa Hoseya, “Ndawalikha . . . (Tsono mvetsetsani, Akulankhula kwa Aisraeli.) . . . Ndawalikha . . .” Kapena kuti “Ndawadula - kuwadula iwo ndi aneneri.” Ndi m’mene Mulungu amachitira ndi anthu ake. Anawadula pakati pa mitundu yina. Ndi chiyani? Lupanga Lake lakuthwa konsekonse, Mawu Ake. Amawadula, mtundu Wake pakati pa mitundu. Anadula mtundu Wake pakati pa mitundu ndi aneneri, Mawu Ake otsimikiziridwa. Kotero wadulanso Mkwatibwi Wake pakati pa zipembezoni ndi Mawu Ake olonjezedwa ndi Malaki 4 m’masiku otsiriza. Kudula Mkwatibwi Wake, kumulikha iye pakati pa mipingo yonse, analikhamo Mkwatibwi Wake.

79 Anadula aneneri Ake - ndi aneneri Ake ndi Mawu Ake, kudula Israeli. “Dzipatuleni nokha pakati pao.”

Taonani . . . Pamene anafuna kuchita ngati ena onse, anadza kwa m’neneri Samueli. Iye anati, “Ndinayamba ndatengapo ndalama yanu? Ndinayamba ndalankhulapo chinachake kwa inu mu Dzina La Yehova ndikusachitika?”

Iwo anati, “Ayi, ndi - ndizokhoza zimenezo, komabe tikufuna mfumu.”

80 Ndi momwemo m’mene mipingo yachitira. “O, timakhulupirira Mawu Ndi Abwino; koma mukudziwa, amati tichite ichi.” Sindisamala chimene akunena, Mawuokha ndi okhoza. Kudikirira. Wawadula iwo kupyolera mwa aneneri.

81 Kodi ndi nthawi yanji iyi, m’bale? Kodi ndi nthawi yanji iyi, atumiki? Kodi mukuona nthawi ya tsiku ndi chizindikiro cha m’mene mukukhalamo? Kodi mukhoza kuchimvetisa? Kodi mukuchiona?

82 Kulikonse tsopano kulibe chitsitsimutso. Aliyense akudandaula, atumiki akulira. Ndinali kuwerenga imodzi mwa - manyuzipepala otchuka imene imadza kuno ku mpingo, nyuzipepala yabwino kwambiri. Ndipo ndimamudziwa mkonzi wake, ndipo ndimawadziwa anthu ake. Ndipo ndi anthu opembeza, abwino, M’bale ndi Mlango Moore, Liwu la Kudza Kwake, imodzi ya manyuzipepala abwino amene akuwerengedwa, Liwu la Kudza Kwake. Koma sangasindikize chinachake pokhapokha chikhale chonena za, “Kusala, kupemphera, kusala, kupemphera! Kuomba lipenaga! Ko . . .” Ndi angati amene amaiwerenga? Mukudziwa, nthawi zonse mumaona. “Kusala, kupemphera, kusala, kupemphera!” Ndi zokhazo mumazimva. “Kusala, kupemphera! Tizakhala ndi kudza kwakukuru kwa tsiku! Pali chinthu chachikuru chimene chidzachitike! Nonsenu pempherani, pempherani pempherani! sitinachedwe aye!

<sup>83</sup> Chifukwa chiyani amachita zimenezo? Chifukwa chiyani amachita zimenezo? Akufuna kudzuka kwakukuru. Akulira, kukhulupirira kuti kudzakhala kudzuka. Ndi anthu abwino. Chifukwa chiyani? Achita chiyani? Sanazindikire kudzuka kwa Mkwatibwi. Mukuona? Ndi chimene chikuwapangitsa kumva momwe akumvereramo. Akudziwa chinachake chiyenera kuchitika; koma taonani, akuchiyang'anira kutali kutsogolo kukubweraku, pamene chachitika kale mwa inu.

<sup>84</sup> Ndi chinthu chomwecho anachichita m'masiku akalewo. Anali kukhulupirira mwa Mesiya alinkudza. Anakhulupirira kuti adzakhalapo wakudza patsogolo pake. Koma zinali pa iwo ndipo sanakhulupirira kuti padzakhala wakudza patsogolo amene adzadza patsogolo pa Mesiyo. Ndipo anamudula mutu wake, namupha Mesiya, chifukwa zinaneneredwa kuti adzachititsidwa khungu. Hoseya anatero.

<sup>85</sup> Ndipo Mzimu Yemweyo amene analankhula kwa Hoseya analankhula kudzera mwa Yohane, ndipo Anati mpingo m'masiku otsiriza ano udzakhala wamariseche ndi wakhungu, ndipo udzamuika Iye kunja kwa mpingowo. Analephera kuona mauneneriwo akukwaniritsidwa. Koma pokhala momwemo akuzindikira kuti chinachake chiyenera kuchitika. Sakuchimvetsa. Sakuchizindikira. Monga ngati Ayuda a nthawi yakale, Laodikaya wakhungu - chuma, maphunziro a chipembezo, olusira mpingo, odana ndi Uthenga. Taonani m'mene Ayudawo anamudera Yohane. Taonani m'mene anamudera Yesu, pamene Iye anali yemweyo amene iwo anali kutsimikizira kuti anali kumuyembekezera. (Fiyuzi ya magetsi ikuphulika mu Branham Tabernacle - mkonzi.) Ndikukhulupirira taphulitsa fiyuzi. Ndikuganizira chimenecho chazimitsanso ma tepi rekoda. Sichitha chabwino.

<sup>86</sup> Anali odana ndi Uthenga . . .

Chimene chinachitika ndi - kuchuruka mphamvu yoyendera . . . Aliyense wa inu ndi chida chotenthetsera. Palibe njira yokhazikitsira mpingo kukhala monga m'mene ungakhalire . . . mu nthawi imeneyo, chifukwa mukuona, aliyense wa inu ali 98 B.T.U.'s m'mene angakhalire. Ndipo sikuti mumangokhala pamene ngati choncho; mumaturutsa kutentha nthawi zonse. Tsopano muli mpweya wokwanira muno kuziziritsa malo ano, koma ndi chinthu chotenthetserachi chikugwirabe ntchito si - simungathe kutero.

<sup>87</sup> Zindikirani. Olusira, koma tsono monga Ayuda akale, achititsidwa khungu; ali ku Laodikaya. Ali amariseche, ochititsa chifundo, atsoka, ndipo osadziwa chimenechi. Tsiku la chuma, maphunziro a chipembezo opambana, maphunziro opambana, ndipo tsono akhala olusira Uthenga. Alibe nao ntchito, monga ngati m'mene zinakhalira mu nthawi imene Yesu wa ku Nazarete anali pa dziko la pansu.

<sup>88</sup> Chifukwa chimene anthu mu tsiku la Nowa sanalowe mu chingalawa - chifukwa sanauzindikire uthengawo ngakhale mthengayo. Ndi chifukwa chokhacho chimene anaonongekera, ndi chifukwa chakuti sanazindikire ora limene anali kukhalamo. Sanazindikire kuti Mulungu adzachita ndi tchimo monga m'mene analonjeza kuti adzachita. Adzaononga munthu pa dziko lapansi. Anachinenera. Anachitsimikiza. Ndipo akuchitsimikizira lero momwemo anachitira nthawi imeneyo.

<sup>89</sup> Koma anthuwo m'malo momuchitira chifundo Nowa... Anamuganizira kuti ndi munthu wosokonezeka. Sanamukhulupirire iye kukhala m'neneri. Mukudziwa, Yesu, Iye Mwini anatiuza m'mene ananyozera mu nthawi ya Nowa, kumuseka, namutchula wojijirika pa zinthu zolakwika, nanga china nchiyani. Koma sanazinkikire nthawi yawo. Sanalizindikire tsikulo. Sanacizindikire chizindikirocho. Sanauzindikire Uthengawo. Sanamuzindikire mthengayo, koma anamuchotsa pakati pawo namuseka. Yesu anati, "Monga m'mene kunaliri mumasiku a Nowa..."

<sup>90</sup> Israeli pokhala mu dziko mwake ndi chirichonse kukhazikika tsopano, ndipo uthenga ukungolowa mwa ngwiro, ndi tsiku lanji limene tikukhalamo, m'bale? Tikulingalira chiyani?

<sup>91</sup> Sanalidziwe tsikulo. Sanalidziwe. Ndi chifukwa chake anaphonya, ndi chifukwa chakuti sanazindikire. Anali ngati tsiku - kukhala ngati anthu lero, achititsidwa khungu ndi zisimikiziro za sayansi, ndi mchitidwe wa maphunziro, ndi maphunziro a zipembedzo. Ndipo zinthu zimene zinawachititsa khungu m'masiku amenewo, zikuwachititsanso lero. Zawachititsanso kachiwiri. Ndiponso kuphweka - kuphweka kwa Uthenga ndi mthengayo.

<sup>92</sup> Nowa sanali wa sayansi, Anali wosaphunzira, anali mlimi wosauka, wodzichepetsa, ndi uthenga wophweka. Unali wophweka kwambiri mofanizira ndi maphunziro awo apamwamba. Chomwechonso lero. Mulungu nthawi zonse amauphweketsa kuti apeze anthu oti angaukhulupirire ndi kumudalira Iye. Ndi wosiyana, wongokhala Uthenga wosiyana, koma Mulungu yemweyo. Ndipo ndikufuna kuti inu mu Ukhulupirire ndi kumvetsa kuti Mulungu wa Ulankhula.

<sup>93</sup> Yesu anati iwo anamunyoza m'neneri Wake, Nowa. Monga m'mene ananyozera m'masiku amenewo, koteronso adzachita chomwecho pakudza Kwake. Adzachita chinthu chomwecho. Ndi chifukwa chake Farao anamira mu nyanja. Sanazindikire tsiku lake. Sanakhoze kuzindikira chimene chinali kuchitika. Anatengeka kwambiri ndi zochitika za mu m'badwo wake wa sayansi kumanga mizinda ndi ntchito ya akapolo. Anata - anatanganidwa kwambiri kotero kuti sanazindikire mwayi umene anali nawo, ndipo anamupititsa m'neneri ndi wamthenga

wa Mulungu mu chipululu. Sanachizindikire. Ndi chifukwa chake zinthu zinayenda momwe zinayenderamo. Sanazindikire. Akanangozindikira Mawu a Mulungu oloseledwa kwa anthu amenewo.

<sup>94</sup> Ndipo mipingo lero ikanangozindikira, ngati mipingo ikanangozindikira Mawu a Mulungu olonjezedwa kwa anthu nthawi ino, sakanaonongeka! Ngati Amerika akanangozindikira chikhazikitso cha boma chimene anayamba nacho, sakanakhoza kufuna kuchotsa ma Baibulo mu masukulu, kuchotsa dzina la Mulungu pa ndalama, ndi kufunafuna kumvera Mulungu. Koma sakuchizindikira. Chifukwa chiyani? Ali wakhungu ndi wamariseche. Sangazindikire mwazi wa anyamata ofunikawo amene anafa chifukwa cha mwayi umenewu. Aiwalika; ali pfumbi.

<sup>95</sup> Koma pali Mmodzi amene amakumbukira kukhetsa - mwazi kwa aneneri, mtengo umene unatengera kuubweretsa uthengawu kwa ife lero, m'mene zikwi zikwi anadyedwera ndi mikango poponyedwa mokhala mikango, m'mene anawadulira pakati, kuwotchedwa, kupachikidwa - Mulungu amakumbukira. Mpingo waiwala aneneri ake, sakuwafunanso; amatero. Koma Mulungu amadziwa kuti Ayenera kukhala nawo. Amawalikha anthu ake ndi Mawu Ake. Koma ndi zachikale kwambiri kwa iwo masiku ano. Sakuzindikira. Ndi chifukwa chake ali mu chikhalidwe chimene alimocho. Ndi chifukwa chake ali amariseche, omvetsa chifundo akhungu, atsoka, ndipo sakudziwa, ndi chifukwa chakuti sakuzindikira nthawi imene tikukhalamo. Sakuzindikira.

<sup>96</sup> Mose, anazindikira tsiku lake ndi maitanidwe ake pamene anaona malonjezano a Mawu a Mulungu a tsiku limenelo akutsimikiziridwa. Kotero anadziwa nazindikira kuti anali ndani ndi chimene akanachita ndi Mawu a Mulungu olonjezedwa. Kotero sanaope chimene wina aliyense ananena. Sanachite manyazi ndi uthenga wake ngakhale wansembe aliyense ndi Farao aliyense, chirichonse, ulamuliro uliwonse, sanagwirizane naye. Koma anazindikira pamene anaona Kuwala kuja, Lawi la Moto lija liri pa chitsamba paja ndi kulankhula kwa iye Mawu amene analonjezedwa mu tsiku limenelo, Ndikuti, "Ndakuyitana pita kachichite." Sanaope zoopseza zazikuru za mfumu. Anapita kukaturutsa anthu amenewo monga m'mene Mawu a Mulungu analonjezera.

<sup>97</sup> Kuona lonjezano likutsimikiziridwa, anawapangitsa anthu kukhonzekera kuturuka kwao. Liti? Pamene anawona lonjezano la Mulungu likutsimikiziridwa. Kumbukirani, anathamanga ndi maphunziro ake a chipembezo; anathamanga ndi kuphunzitsidwa. Koma pamene anawona Mawu a Mulungu akuonetseredwa, anawona akutsimikiziridwa, "INE NDI INE AMENE NDIRI," kotero sanasamalire zonena za wina aliyense. Sanawope chimene ena onsewo akanachita. Anangoopa

Mulungu, kuti mwina sangamumvetse Mulungu, kapena njira ina yoti sangamumvetse nayo Mulungu. Sanawope anthu ndi chimene akananena kapena kuchichita. Anangoopa Mulungu atazindikira kuti anali Mawu a Mulungu.

<sup>98</sup> Sanakhoze kumvetisa mmene munthu ngati iye akhoza kutumidwa kumeneko. Koma pamene anazindikira ndi Mawu otsimikiziridwa a chimene chinali, kotero sanawope malamulo a mfumu. Mukanangozindikira. Ngati ife lero tikanangozindikira! Mose anazindikira pamene anawona Mawu akutsimikiziridwa, anawona kutsimikizira kukuchitika...?...Anali wokonzekera kuwatulutsa anthuwo.

Yobu sanazindikire kuti anali Mulungu. Ngati satana angakhoze - angakhoze kukupangisani inu kukhulupirira nthawi zina kuti mayeso aang'ono amene mumapitamo ndi - ndi Mulungu akukusausani...Anali Mulungu akuyesa kumuonetsa china chake. Yobu sanazindikire mpaka pamene anawona masomphenya monga Mose. Pamene Mose anawona masomphenya, Lawi la Moto mu chitsamba, chimatsimikizidwa. Ndipo pamene Yobu mu funso lake: “Ngati munthu afa, azakhalanso ndi moyo? ndimawona mtengo ukafa, umakhalanso ndi moyo ndimawona duwa likafa limakhalanso ndi moyo. (Limenelo linali funso lake.) Koma munthu amagona, amapereka mzimu, nataika. Ana ake adza kudzalira, ndipo iye samawona, O, kotero mudzandibisa ine m'manda mpaka mkwiyo wanu utapita.” Sanakhoze kumvetisa chifukwa chiyani duwa likhoza kufa ndi kukhalanso ndi moyo, chifukwa chiyani tsamba likhoza kugwa mu mtengo, pansu, ndi kukhala pa dothi, ndi ndikubwereranso m'nthawi ya dzinja. Anati, “Munthu amagona, nanga amapita kuti? Ndikukhulupirira Mulungu; koma chimachitika kwa munthu ndi chiyani?”

<sup>99</sup> Koma tsiku lina mphenzi inayamba kung'anima mabingu anayamba kugunda, Mzimu anadza pa m'neneriyo, ndipo anawona kudza kwa Munthu amene anakhoza kuika dzanja lake pa munthu wochimwa ndipo Mulungu Woyera nalumikiza njirayo. Kotero anafuula, “Ndikudziwa Mombolo wanga ali wamoyo! ngakhale mphutsi zitaononga thupi ili koma mu thupi langa ndidzamuona Mulungu!” Anazindikira chimene chiukitso chinali.

<sup>100</sup> Balaamu sanamzindikire Mngelo mpaka pamene bulu analankhula m'malilime. Balaamu sanakhoze kuzindikira kuti Mngelo anayima patsogolo pake. Mlaliki wochititsidwa khungu sanakhoze kuzindikira kuti anali Mulungu amene anayima patsogolo pake kuyesa kumuletsa iye kuti asagulitse mphatso yake chifukwa cha ndalama. Ndipo pamene bulu analankhula ndi mawu a munthu, kenaka Balaamu anazindikira kuti anali Mngelo amene anayima patsogolo pake kuyesa kumuletsa iye asachite chimene anali kuchita.

<sup>101</sup> O, azipembezo akhungu inu, ngati Mulungu angakhoze kugwiritsa ntchito bulu wosalankhula kuti alankhule chinenero chimene sakuchidziwa kuululira mtumiki kuti wasiya njira, kodi sangakhoze kumugwiritsa ntchito munthu kuti achite chimenecho. Anthu a khungu.

<sup>102</sup> Ngati Ahabu akanangozindikira tsiku lake sakanamutsutsa m'neneri Mikaya ali ndi Mawu a Mulungu olonjezedwa kwa iye.

<sup>103</sup> Pamene Ahabu anaima pamenepo tsiku limenelo, iye ndi - ndi Yehoshafati...Ndipo pamene anali ndi aneneri mazana anayi pamenepo akunenera, nanena, "Pitani, zonse ziri bwino. Ahabu ukukhala m'machimo. Munatipangira ife mpingo waukuru; ndife anthu apamwamba; ndife utumiki wapamwamba. Tadza; tiri ansembe ophunzitsidwa mazana anayi - kapena aneneri. Tiri mazana anayi ophunzitsidwa m'Mawu ndi maphunziro a zipembedzo. Tikudziwa zonse." Koterotsonochinatsimikiziridwa kuti sanadziwe zonse.

<sup>104</sup> Munthu amene anamutchula kuti wosokonezeka mu m'bado umene unali pambuyo pawo Eliya, m'neneri woona wa Mulungu, amene ananenera, "ATERO AMBUYE, agaru adzanyambita mwazi wako, Ahabu!"... Mukuona?

<sup>105</sup> Koma ansembe amenewo, aneneri opangidwa ndi anthu, anaganiza kuti anakhazikitsa zonse bwino. Anati, "Atate Abrahamu - kapena Atate Ahabu, pitani, Ambuye ali nanu. Muli nao Malembo, chifukwa Mulungu anapereka dziko ili kwa Israeli. Ndi la Israeli. Pitani, Ambuye ali nanu." O, mayi!

<sup>106</sup> Koma mukudziwa, Yehoshafati, amene sanasakanikirane mu tchimo ngati Ahabu, anawona zinthu kusiyana pang'ono. Anati "Kodi palibenso wina?"

<sup>107</sup> Anati, "Tiri naye m'modzi pano, koma ndimamuda" Mukuona? Kodi Mulungu anali kuchita chiyani? Kudulanso anthu ake ndi m'neneri. "Ndimamuda iye. Samachita chiri chonse koma kunditsutsa nthawi zonse. Ndipo mukudziwa ndine munthu wopambana. Sindikanakhala ndi seminare iyi pano ngati sindiri wokhulupirira kopambana. Ndiri ndi anthu ophunzitsidwa bwino. Ndimawakhazika pamenepo ndi mabuku, ndi mabaibulo, ndi zina zonse kuti aphunzitse chimenechi. Ndipo ndikudziwa kuti ndi anthu opambana." Koma ngati Ahabu akanangozindikira kuti munthu ameneyo anali ndani, munthu uyu wooneka wosauka, mwana wa Imlah, akuima pamenepo namuza "ATERO AMBUYE," sakanachita kulakwa koopsa kumene anachitako. Koma anamutsutsa Mikaya. Sanachite...

O, anthu inu, zindikirani mbado umene mukukhalamo! Tawonani chimene chikuchitika, Tawonani, chimene chalonjezedwa. Zindikirani tsiku limene mukukhalamo.

<sup>108</sup> Ngati zipembedzo zikanangozindikira chifukwa chiyani zikutsutsidwa ndipo mamembala awo akuwathawa monga

Israeli kuturuka mu Aiguputo, ngati zipembezdo zikanasiya kutsutsa ma tepiwo ndipo kumangowamvetsera iwo... Ndipo inu, alaliki, mvetserani ku tepi iyi, mvetserani. Mukanangozindikira nthawi imene mukukhalamo, mukanangozindikira chizindikiro cha nthawi, mukanawona chifukwa chimene anthu akumathawa zipembezo. Mzimu wa Ambuye ukuitana... "Palibe munthu adza kwa Ine," anatero Yesu "Pokhapokha Atate atamukoka iye. Ndipo onse amene Atate anandipatsa Ine, adzadza."

<sup>109</sup> Monga mkazi wa pachitsime, ndi wansembe, m'mene anakhalira osiyana. Dzanja lolemba liri pa khomanso la lero. Akuliwona, koma sakulizindikira.

<sup>110</sup> Ngati Ayuda akanangozindikira chizindikiro cholonjezedwa cha Mesiya wao monga mwa mneneri wao wotsiriza; Malaki 3 anati, "Tawonani, Nditumiza mthenga ndisanaonekere Ine ndipo adzakonza njira." Ndipo amanena motsimikizira kuti anali kumuyembekezera Iye. Ndicho - ndizofanana chimodzimidzi mpaka-lero.

<sup>111</sup> Akunena motsimikizira kuti akuyang'anira china chake kuti chichitike. Mipingo yonse ikupemphera ndi kusala, ndi kuti, "Tsono, tiyeni tipemphere. Tiyeni tikhalire palimodzi. Tiyenera kukhala ndi chinthu chopambana choti chichitike. Tikudziwa pali chinthu china chake chopambana choti chichitike; mpingo uyenera kukonzeka." Ndi chimene akupempherera.

<sup>112</sup> Ndi chimene anali kuchipempherera. Ndipo anadza Yohane M'batizi. Chifukwa anakana ma seminare awo, chifukwa anachita zotsutsana ndi zimene makolo awo anaphunzitsa... Anadza kuchokera ku chipululu wopanda maphunziro. Anadza wopanda kolala yake yotembenezidwira kumbuyo, monga m'mene akanafotokozera masiku ano. Anadza wopanda chimulu cha maphunziro a zipembezo; koma anadza modziwa malonjezana a Mulungu kuti anali woti amulengeze Mesiya. Anati, "Wayima pakati panu tsopano." Koteri anaganiza kuti iye anasokonezeka chifukwa sanali wochokera ku sukulu zawo. Dzanja lolemba linali pa khoma, koma sanazindikire. Ananena motsimikizira kuti anali kuyang'anira munthu ngati ameneyo kuti adze; ndipo anali pakati pawo pomwepo; ndipo sanazindikire, ngakhale ananena kuti anali kumuyembekezera Iye.

<sup>113</sup> Chimodzimidzi monga Ayuda kuti anali kudya ndi Amitundu a pa dziko, chifukwa chinaneneredwa chinthu chomwecho, motero. Ananena motsimikizira kuti anali kumuyang'anira Iye. Koma zipembezo tsopano mu m'bado wa Laodikaya wa Amitundu wangokhala wakhungu ngati m'mene iwo anakhalira. Chifukwa chiyani? Zinaneneredwa kuti adzatero. Ziyenera kuchitika.

114 Ngati a Israeli akanangozindikira chizindikiro chawo, akanadziwa kuti nthawi yoonekera Mesiya inafika. Akanangozindikira . . . Mukudziwa o - phunzira ananena chimenecho kwa Yesu, “Chifukwa ninji alembi amati Eliya ndiye atsogole kudza?”

115 Ndipo Yesu anati, “Eliya anadza kale ndipo sanamudziwe iye.” Anakhala pano kale, ndipo amupha kale. Anachita chomwecho chimene Malembo ananena kuti adzachita.

116 Akanangozindikira kuti munthu wojjirika pa zolakwika ameneyo amene anawatsutsa pa zinthu zophatikiza zonse zimene anachita, anatsutsa zinthu zonse zimene anali kuchita . . . Anati, “Anthu onyenga inu, musayambe ku . . . anthu odzibisa, obadwa a njoka inu, wakuchenjezani ndani kuthawa mkwiyo uli nkudza? Musayambe kuganiza mwa inu nokha ‘Tiri naye Abrahamu tate wathu; tiri ndi izi, izo, kapena zina zake;’ pakuti ndinena kwa inu, Mulungu akhoza kuukitsa miyala iyi ikhale ana kwa Abrahamu.”

117 Musayambe kuganiza kuti muli ndi bungwe la dziko mmanja mwanu, ndipo muli ndi mamembala obvala bwino a . . . Mulungu akhoza mwa anthu osokonezeka awa kuukitsa ana kukwaniritsa Mawu Ake-mahule, anthu ongoyendayenda mu mseu, oledzera, a juga. Akhoza kuchita chimenechi. Ali Mulungu mpaka pano.

118 Azipembezo akhungu monga Israeli wakhungu, onse ananeneredwa kuti adzakhala chomwecho. (ndikukuonetsani zofanana mpaka nditafika pa malo awa amene ndikufuna tsopano) Akhungu, monga zi - zipembezo za Amitundu a m'bado wa Laodikaya ndi za khungu lero monga m'mene anakhallira nthawi imeneyo.

119 M'bado wa Laodikaya uyenera kulandira uthenga; Malaki 4 anati adzatero. Koma akuyang'anira chiyani? “Chipembezo chathu chidzaonetsera. Ndipo ngati sichidza kudzera mwa ife, a Baptist, a Presbyterian, a - a Assemblies, a oneness kapena a - ngati sitichiwonetsera chimenechi, si chowona.” Chomwecho chimene anachita m'masiku amenewo. Ndipo chinadza ndi kupita ndipo sanadziwe. Sanachizindikire ngakhale chinakwaniritsa liwu liri lonse. Yesu anati, “Anachita monga m'mene anafunira. Kotero adzatero nayenso Mwana wa munthu. Adzakanidwa.”

120 Tsono zindikirani. Chomwechonso m'masiku a Amitundu, monga mwa Malembo olonjezedwa a pa Malaki 4; amene Yesu anati “Malembo onse anauziridwa, ndipo palibe ndi pang'ono pomwe amene sadzakwaniridwa. Ndipo Yesu anati zidzachitika. Ndipo pano tikuona zachitika. Tikuona.

121 Kubwezeretsa chiyani? M'masiku ano otsiriza . . . Inu abale a mzipembezo, mvetsani. Kubwezeretsa phwando la Pentekositi la pa chiyambi monga m'mene zinakhallira pa chiyambi: Kotero lidzabwezetsedwa lisanalire Lipenga la phwando la Israeli,



liyenera kubwezeretsedwa. Payenera kukhala china chake choti chichite chimenecho. Malaki 4 anati chidzabwezeretsedwa chimene chidzachitika . . .

<sup>122</sup> Ngati Israeli akanangozindikira Mesiya wao, chizindikiro cholonjezedwa, sakanakhala pamene ali lero. Akanango . . . Koma chifukwa chiyani sanachite chimenecho? Ndi zomvetsa chifundo. Chifukwa chiyani sanachite chimenecho? Chifukwa Mulungu ananena kuti sadzachita chimenecho. Ndi angati amene akukhulupirira chimenecho, anene “Amen.” (Gulu libvomera “Amen”—Mkonzi.) Mulungu anati sadzachita chimenecho. Ndipo ndi Mulungu yemweyo amene anati zidzachitikanso mu m’bado uno wa Mpingo wa Laodikaya; ndipo pano ziri pamaso pawo. Angachite bwanji chinachake chosiyana ndi chimenecho?

<sup>123</sup> Akanangozindikira chizindikiro cholonjezedwa cha Mesiya, chizindikiro cha Mwana wa munthu. Iye anadza mu dzina la Mwana wa munthu. Tsono, anali mu dzina mu m’badwo wa Pentekosite, mwa Mzimu Woyera, Mwana wa Mulungu. Tsono, chotsatira ndi zaka chikwi, Mwana wa Davide. Ana atatu - Mulungu yemweyo. Atate yomweyo, Mwana, Mzimu Woyera; Mulungu Yemweyo. Mwana wa Davide, Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu ndi Mulungu yomweyo nthawi zonse mu ma ofesi antchito atatu osiyana.

<sup>124</sup> Koteri ali Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, osakhala milungu itatu, koma Mulungu Yemweyo mu nyengo zitatu, maofesi atatu a ntchito, monga Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Koma monganso lero, achitisidwa khungu ndi miyambo monga anachitira iwo, achita khungu ndi Miyambo, sakuwona. Chifukwa chiyani sakhoza kuwona? Sadzawonanso. Kumbukirani, chimenecho ndi ATERO AMBUYE. Mukuti, “Nanga chifukwa chiyani mukuchilankhula?” Momwemo m’mene Yohane anachitira, momwemo m’mene ena onse anachitira. Alipo ena amene akanirira apa ndi apo amene ayenera kuturutsidwa. O, nkhosa za Mulungu, imvani Liwu la Mulungu! “Nkhosa zanga zimamva Mawu Anga.”

<sup>125</sup> Mzimayi wa pa chitsime anazindikira tsiku lake ndi chizindikiro cha Mesiya. Anali m’maonekedwe oyipa. Sanafune kumapusa ndi mipingo ya kaleyo monga momwe anali kuchitira. Anali kukhala mchikhalidwe chiri chonse, ndi zinthu zimene anali kuchita. Iye sanakhulupirire mu zinthu zimenezo. Koma anadziwa adzadza Wina tsiku lina. Kamunthu kovutikaka pa njira yake yopita ku chitsime anachipeza chimene anali kuchiyang’anira pamene Iye anayamba kuulula zinsinsi za mtima mwake, anamuuzza za tchimo limene anali kukhalamo. Iye anati, “Bwana ndikuzindikira kuti ndinu Mneneri.” (Tsono, analibe mneneri kwa zaka mazana anayi) Anati, “Ndikuzindikira kuti ndinu Mneneri. Ndipo ndikudziwa kuti

akadza Mesiya Adzachita zinthu zimenezi.” Iye anati, “Ndine amene.”

<sup>126</sup> Anazindikira. Panalibenso funso lina. “Mungachitsimikizire bwanji?” Chinatsimikiziridwa kale. “Ichi ndi chimene adzachita Mesiya akadza.” Chabwino, ngati akhoza kuzindikira mwa Malembo, sitingakhoze ife kuzindikira Kuwala kwa madzulo ndi chizindikiro cha tsiku la lero? “Tikudziwa akadza Mesiya Adzationetsa ife zinthu zonsezi. Iye adzatiuza chimenechi.” Iye anati, “Ndine amene ndikulankhula nawe.”

<sup>127</sup> Panalibenso funso lina. Anachoka pamenepo. Ndipo anawafotokozera anthu, “Bwerani mudzamuone, Iye ali kuno!” Panalibenso funso lina kwa iye. Chinakhazikitsidwa, chifukwa anazindikira tsiku limene anali kukhalamo. Anazindikira.

<sup>128</sup> Koteronso Natanieli, M’Heberi wopambana. Pamene anawona chizindikirocho cha Mesiya chimene chinalonjezedwa kumeneko, zinalibe kanthu khaya ansembe angati, khaya china chiri chonse... Chinachita chiyani? Chinasokoneza ansembe powona anthu akusiya mipingo yawo ndi kumapita. Anati, “Ngati wina wa inu akakhala nawo pa msonkhano Wake mudzachotsedwa. Tidzakuponyani kunjira kwenikweni kwa chipembezo.”

<sup>129</sup> Koteronso lero. “Tikuchotsa mu bungwe lako ngati ukakhala nawo pa msonkhano wake.”

<sup>130</sup> Mukumukumbukira munthu wakhungu uja? Atate ake ndi mayi ake sanakhoze kuyankha. Anachita mantha chifukwa anati aliyense amene anapita kukamuwona Yesu kapena - kapena kukhala nawo pa msonkhano Wake, adzachotsedwa. Koma munthu wakhunguyo anakhoza kudzilankhulira yekha. Iye amene anali wa khungu nthawi ina anakhoza kuwona.

<sup>131</sup> Ine amene ndinali wakhungu nthawi ina ndikukhoza tsopano kupenya. Ine amene sindinadziwe zinthu zimenezi, zadziwitsidwa kwa ine ndi Mzimu Woyera. Masulani zipembezo, chifukwa akudzabe!

<sup>132</sup> “Ndikadzakwezedwa kuchokera pa dziko, ndidzaitanira anthu onse kwa Ine.” Natanieli anachizindikira; anadziwa.

<sup>133</sup> Monganso Mose, zotsimikiziridwa ndi Malembo, Mawu otsimikiziridwa; Mose anadziwa kuti ilo linali lonjezano la tsiku limenelo, chifukwa zinagwirizana ndi Malembo. Zinalibe kanthu kuoneka za chilendo... Iye anati, “Ndikawauza kuti ndi ndani...? Ndiwafotokozera ndaona Kuwala mu chipululu. Ndiwafotokozera bwanji tsono kuti kunali Kuwala kwandekha kuno, ndipo Kuwala kumeneku kwandiuza kuti ndipite kumeneko?”

<sup>134</sup> Iye anati, “Zoonadi, Mose ndidzakhala ndi iwe.” Ndipo osangokhala... Sanangodziwonetsera Iye Yekha mu Iguputo mwa zozizwitsa ndizizindikiro, koma pamene

anawasonkhanitsa iwo pamodzi anaonekeranso kwa iwo, ndi kutsimikizira utumiki wa Mose pamaso pa osankhidwa ndi oitanidwa. Pamene mneneriyo anawadula, kuwamasula ku dziko kuwabweretsa iwo pa malo, kotero Lawi la Moto linaonekeranso pamwamba pa Phiri la Sinai. Zolinganananso ndi lero. Amen! Alemekezeke Mulungu! Ndi choposa moyo kwa ine.

<sup>135</sup> Monga m'mene msinkhu wanga ukupitirira ndipo ndikuona nthawi ya zonyansa ndipo zosayenera zikukwana pa dziko, ndi zina zonse, kotero ndimayang'ana pambuyo ndi kuwona chimene chachitika; mtima wanga umadumpha ndi chimwemwe, kudziwa kuti patapita kanthawi kachisi uyu wokhalamo pa dziko lapansi adzatha, koma pali wina amene akundiyebekezera kumeneko. Ndikuyetsetsa kukoka anthu, kuwakula ku zinthu izi ndi izi, kuwakokera kunja kuwaonetsa ndi Malembo kuti Mulungu waima pamenepo ndi chitsimikiziro cha Lawi la Moto limene mazana mazana ndi zikwi zikwi analiwona nalijambulanso ngakhale ndi chojambulira zithunzi nthawi ndi nthawi kutsimikizira.

<sup>136</sup> Anthu ongochita zinthu mowonera alipo. Indedi, ziyenera kuchitika. Anthu ongochita zinthu mowonera analipo m'masiku a Mose ndipo anachita zofanana chomwecho. Mulungu anati, "Udzipatule wekha, Mose. Usakhale pafupi nawo. Ndiwamiza!" Ndipo dziko linawamiza. Koteronso ziripo lero. Tabwererani mu dziko mwenimweni - njira zopezera ndalama, ndi zina zonse. Mukuona?

<sup>137</sup> Chizindikiro cha Malembo cha Mose... Adali - adali mneneri wopambana wa Mulungu amene adapita kumeneko kukawapulumsa. Ndipo iwo adazindikira; adazindikira chizindikirocho. Linali lonjezanso lenileni la Malembo, lotsimikiziridwa.

<sup>138</sup> Yesu anali lonjezanolo la m'Malembo, lotsimikiziridwa kwa mzymayi. Kapena titi Anali Tanthauzo. Yesu anali Yanthauzo la Malembo, Moyo Wake womwe unatanthauzira Malembo.

<sup>139</sup> Kodi simukuona uthenga wa nthawi iyi? Kodi mungazindikire pamene tiri? Uthengawu uwo wokha wochokera m'Malembo ukutanthauzira kwa inu nthawi imene ife tikukhalamo. Ndi tanthauzo.

<sup>140</sup> Yesu anati kwa Israeli, "Mukanangodziwa tsiku lanu." Tsiku lina atakhala pa phiri la Azitona anayang'ana, nati, "Yerusalemu, O, Yerusalemu..." Analira. Anayang'ana pansu; Anawona... Osakhala mofananitsa kapena mwina - usiku wina - mmawa wina cha m'ma teni koloko pamene ndinawona mpingo uja wa chigololo. Mkati mwa mtima wanu munamva Mzimu Woyera ukukulirirani. "Yerusalemu, O, Yerusalemu, ndi kangati kamene ndingakufungatireni inu. Koma munachita chiyani? Munapha aneneri amene ndinawatumiza kwa inu. Munawapha iwo!" Kotero mauthenga otumizidwa ku mipingo

lero aphedwa ndi zikhulupiro za zipembezo zao. Malembo aphedwa ndi zikhulupiro zawo. Yesu anati, “Mukanangodziwa tsiku lanu; koma ndi kutali kwambiri tsopano. Nthawi yatha kwambiri tsopano.” Koteronso ziri chomwecho ndi mipingo.

<sup>141</sup> Ndimakhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti apyola poti angawomboledwe. Ziribe kanthu mukuganiza motani, amenewo ndi maganizo anu, awa ndi anga. Mukuona? Simukukakamizidwa kutsata maganizo anga. Mukuona? Koma ine ndikukhulupirira kuti wapyola poti ungawomboledwe, ndipo kwapita zaka zisanu kapena zisanu ndi chimodzi. Ine ndikukumbukira - Inu mukukumbukira ku Chicago. Onani zimene zinachitika kuyambira nthawi imeneyo, ndipo onani kuti zakhala zikuchitika. Mukuona? Kumbukirani, dzina langa liri poyambirira pake, zinakhomedwa pamenepo, ndi ATERO AMBUYE. Onani ngati sanakhale akugwa mopitirira.

<sup>142</sup> Tayang’anani mu chaka 1933: momwe anati azimayi azidzachita motere m’masiku otsiriza; momwe anati kwa anthu...momwe Mussolini, momwe akanadzathera; momwe Hitler akanadzathera mosadziwika; momwe makhalidwe atatu amayiko akanadzagwirizanira ndikulowa mu chikominisiti; momwe kudzapangidwe magalimoto owoneka ngati dzira; ndi momwe azimayi azidzavala zovala zofanana ndi amuna ngakhale zofanana ndi zovala zawo za mkati, ndi kuti adzafika pomadzavala zokhala ngati masamba a mkuyu; momwe chiwerewere, momwe azidzachtira m’masiku ano. Penyani zomwe ayamba kuchita. Ziri pa maso panuno.

<sup>143</sup> Ngati azimayi a Chikhristu akanango (awo amangochedwa alongo a Chikhristu) - akanango - zindikira, akanangozindikira kuti mzimu umene ukuwachititsa zosayenera ndi wa satana kuwapangitsa iwo kumeta tsitsi lao. Ndi Satana yekha amene angachite zimenezo. Ndi zosiyanana ndi Mawu a Mulungu kwa inu. Monga mmene zinakhallira m’unda wa Edeni. Kodi achita...? Akanangozindikira. Amayesa kunena, “O, ka mlaliki kotengeka kaja kakuti...” Sindine, Sindikukuuzani choti muchite. Ndikungobwereza Mawu. Akanangozindikira kuti ndi Satana.

<sup>144</sup> Amadzitchula okha Akhristu. Yesu anati, “Munganditche bwanji Ine, Ambuye, ndi kusachita zinthu zimene ndikunena kuti muchite?” Sangakhale Akhristu. Ine si woweruza wao, koma ndikungolankhula chimene Mawu amanena. “Munganditche bwanji, Ambuye, ndi kusamachita zomwe ndinati muzichita?” Ndipo Mawu onsewa pano ndi bvumbulutso la Yesu Khristu. “Inu mukunditcha Ine, Ambuye, ndani?”

<sup>145</sup> Akanangozindikira kuti ndi Satana, mzimu wachiwerewere. Tazimayi tina tabwino tiripo uko. . .

<sup>146</sup> Ndikuganiza kuti ano ndiwo malo oyipitsitsa amene ndawaona m’moyo mwanga, Jeffersonville, Indiana, pa nkhani

ya azimayi amariseche. Ndakhalapo ku Hollywood; ndakhala kwina konse; ndakhala mu dziko lonse lapansi, ndipo ndaona zonyansa za mitundu yonse. Ndawona ku Paris; Ndaona ku England, kumene kuli ku likulu la onsewo.

<sup>147</sup> Ndikuganiza kuti England anayenera kumizidwa pansu pa nyanja; ayenera kutero. Zonyansa, zoipa, zosayenera... Ndi ku chithaphwi cha za ubve za dziko lapansi, anthu okanitsitsa za Malembo amene ndawaona mmoyo mwanga. Wakhala chomwecho, chifukwa wakana Choonadi.

<sup>148</sup> Billy Graham anati anamchotsa mkazi wake ku ma park - amuna ndi akazi, anyamata ndi atsikana akungogonana mu park, poyera. Asandulika malo aubve. Koteronso France; koteronso dziko lonse lapansi; koteronso United States akusandulika mtsogoleri wa onsewo.

<sup>149</sup> Tawonani lero. Kuwalola akazi kumeta tsitsi lawo, kubvala makabudula, mabuluku, kusuta - ndi kumadzitcha okhulupirira. Kodi simukuzindikira, mlongo, kapena mzimayi... Ndikutanthauza... Pepani... osakhala alongo anga, kuchita zoterozo. Kodi inu simukuzindikira kuti ndi mdierekezi? Koma chiyani... Monga Ayuda akale, simukhulupirira Mawu otsimikizirika pamene atsimikiziridwa kwa inu. Mukukangamira pa miyambo ya zipembezo zanu zikunena kuti ili bwino. Mukulankhula m'malirime, mukudumphadumphira, mukuimba mu uzimu - ndi kumameta tsitsi lanu. Mukuganiza Mkristu angachite zimenezo? Ndawona ziwanda, ndawona asing'anga, ndawona iwo akulankhula m'malirime ndi kuthandauzira, ndi kudumphadumphira ndi kuyima mu uzimu, kumwera magazi mu chibade cha munthu, ndi kumatukwana Dzina la Yesu Khristu.

<sup>150</sup> Mukuti, "Ndine wa mu mpingo. Aleluya! Ulemerero kwa Mulungu! Ine..." Ndinu wa chiyani? Mpingo ndi Mawu ndipo Mawu amati ndi chamanyazi kwa inu kuchita zoterozo! Inu gulu la Afarisi a khungu, kutsogolera tiana ku gehena chotero. Chifukwa mukuopa kulandidwa tiketi ya chakudya, kuti mudzaturutsidwa mu chipembezo chanu ngati muyambitsa chinthu china cha... Mulibe manyazi, inu anthu onyenga! Chitani manyazi! Kumaliwona ora likuyandikira chotere, ndipo nkumapotoloka kuchoka ku Mawu a Mulungu chifukwa cha miyambo yanuyo. Mukulimba mtima bwanji, akhungu inu.

<sup>151</sup> Kodi Baibulo silikunena kuti munachititsidwa khungu? Kodi simukhoza kumvetsa kuti muli akhungu? Baibulo linatero. Kotero muli amariseche, omvetsa chifundo, atsoka, akhungu, ndipo simukudziwa pamene mukuganizira kuti muli ndi mpingo waukuru koposa mu mzindamo, ndipo mukuchita ichi, icho, kapena zina; kotero Baibulo linati muli osauka mmene mungakhalire ndipo muli akhungu. Kotero Yesu Akuimabe pakhomo kuyetsa kukugulitsani mankhwala opaka m'maso -

osakhala kukugulitsani, koma kukupatsani; koma simungathe kulandira. Zikukwaniritsa Malembo.

<sup>152</sup> Ndi tsiku lanji limene mukukhalamo, anthu? Kodi mukuzindikira nthawiye, kuzindikira chizindikiro?

<sup>153</sup> Akanangozindikira, azimayiwo, kuti ameneyo ndi mdierekezi. Ndi mdierekezi wopanda khalidwe mu dzina la chipembezo. Wakhala akukhala mu njira imeneyo. Amadza kwa mneneri aliyense; amadza kwa woyera mtima aliyense; anadzanso kwa Yesu Khristu ngati munthu wopembeza. Kotero Baibulo linati adzakhala chimodzimidzi mmatsiku otsiriza (ngakale achiPentekosite), Kotero kuti adzanyenga osankhidwawo mu mpingo wa Pentekositewo ngati kuli kotheke.

<sup>154</sup> [Mbali yachiwiri iyamba mosakwanira - Mkonzi.] “. . . Koma a pang’ono.” Anati, “chifukwa chipata ndi chopapatiza ndi njira ndi yaing’ono, ndipo ochipeza adzakhala ochepe. Pakuti monga kunali mmasiku a Nowa, Mmene miyoyo isanu ndi itatu yokha inapulumutsidwa, koteronso kudzakhala m’masiku akudza. kwa Mwana wa munthu.” Taganizirani! Ndi tsiku lanji limene ife tikukhalamo? Kodi mukuzindikira nthawi iyi, kuzindikira tsikuli? (Ndikukutengerani nthawi yambiri, koma ndatsala ndi maminiti ochepe.)

<sup>155</sup> Kuwapangitsa iwo kumeta tsitsi lawo. O, akuti, “Mpingo wathu susamalira zimenezi.” Mukudziwa chifukwa chake? Ali akhungu. “Siziri zowopsa kumeta tsitsi lanu.” Baibulo limenena kuti ndi zowopsa! Ndiponso ndi chinthu chosayera, kwa inu ometsa tsitsi lanu lanu, ngakhale kupemphera. Mukuti, “Chabwino, mkazi ayenera kuphimbidwa, osakhala chipewa, tsitsi lake!

<sup>156</sup> Bwanji Mose akanati, “Ndivula chipewa changa m’ malo mwa nsapato zanga?” Chimenecho sichikana chita kanthu. Mulungu anati, “nsapato.” Mulungu anatathauza nsapato. Anati, “tsitsi,” osakhala chipewa! Ulemerero ukhale kwa Mulungu! Anakonda chimenechi, ndikutsimikiza. Matamando akhale kwa Mulungu! Amangothandauza chimene Amachilakhula. Malembo samamasuliridwa mwa mseri. Samangotanthauzira chipembezo chanu chokhacho; Amatanthauza chimene Akunena; ndipo iye ndiye womasulira.

<sup>157</sup> Mukuti, “Ndikudziwa mkazi amene amachita. . .” Sindisamala chimene mukudziwa; ndikudziwa chimene Mulungu analankhula pa chimenecho. Mukungodziyeneretsa nokha.

<sup>158</sup> Akanangozindikira chimenecho chiri, mzimayiyu! Mukanangozindikira nditi mkazi osati mzimayi.

<sup>159</sup> Ndinawona chikwangwani ndikuchokera ku Blue Boar, kutsika, ndikukhulupirira ndi ku Fifth Street kumeneko, pa malo ena ogulitsirapo mowa, anati, Matebulo a azimayi.

Ndinangoima pomwepo...Ndinati, “Simunakhalepo ndi mmodzi yemwe.” Mzimayi sangapite m'malo ngati amenewo; mkazi akhoza, koma osati mzimayi.

<sup>160</sup> Kodi munaonetsetsa kuti kugwa kwa dziko lapansi kumayamba ndi chiwerewere cha mkazi? Kodi mukudziwa kuti ziyenera kuthera mu njira yomweyo, chiwerewere cha akazi. Ndipo mpingo umaimiriridwa ndi mkazi? Mpingo ndi mkazi, ponena za uzimu. Koteronso Mkwatibwi ndi mkazi, ponena mwa uzimu.

<sup>161</sup> Chiwerewere cha Mpingo - m'mene wachitira. Tawonani masomphenya, tawonani zinthu. Tawonani masomphenya, ngakhale amene Mulungu amapereka... Ndipo masomphenyawo ndi owona. Ndiri ndi Baibulo langa pa mtima panga, kwa inu anthu muli pa tepi, alipanowa akuwona. Ndinawona chimenecho! Mulungu Wamphamvu zonse akudziwa kuti ndi zowona zimenezo. Sindinadziwapo mpaka nthawi yomwe ino. Uli wamariseche, ndipo sakudziwa. Unali kungokhala ndi nthawi yake yopambana. Ndi zimenezo. Koma pamene Mkwatibwi wochepe uyo anadza mu kuwonekera, zinali zosiyana. Alefa ndi Omega.

<sup>162</sup> Mdierekezi amatero. Koma monga Ayuda akale, pamene awona Mawu...Ndipo Yesu anati kwa...Anati kwa ophunzira ake: “Fufuzani Malembo. Mu - muku - Muku sokonezeka ndi za Ine ndi Utumiki Wangwa. Fufuzani Malembo; m'menemo mumayesa muli nawo Moyo Wosatha, ndipo amachita umboni za Ine. Amakufotokozerani za Uthenga Wangwa kuti ndi Wotani. Ngati simungandikhulupirire Ine, khulupirirani mawu omwewo amene Mulungu akuwatanthauzira kwa inu.”

<sup>163</sup> Sitingamulole munthu uyu kuti azitilamulira. Tiri nawo ansembe athu ndi ena oterowo. Chabwino pitirizani, tingonena choncho. Nthawi yatha kalebe. Mukuona? Miyambo ya zipembezo imene imanena kuti ziri bwino - amamvera zimenezo. Kukanakhala bwino akanamva...Mudzakhulupirira mawu a - a munthu kuposa m'mene mungakhulupirire Mawu a Mulungu.

<sup>164</sup> Sakuzindikira...Mpingo lero sikuzindikira 11 Timoteo 3. Ngati inu - Ndikuwona ena a inu mukulemba Malembo. Tsono, awa ndi Malembo amene ndikuwakumbukira pomwe pano. Pamene wina akanakhoza kundifunsa, Ine - kapena kuti ndiwalozere zimenezo, ndikhoza kuwawonetsa Lembo lake la chimenecho. Mukuona?

<sup>165</sup> Sakuzindikira 11 Timoteo 3, pamene anati: “Mmasiku otsiriza anthu adzakhala olimbilira, otukumuka mtima, Okonda zokondweretsa munthu osati okonda Mulungu, osayanjanitsika, akudyerekeza, osakhoza kudziletsa, osakonda abwino (mkwatibwi. Mukuona?); akukhala nawo mawonekedwe a chipembedzo, koma m'phamvu yake adayikana: kwa iwonso udzipatule. Pakuti awa ndiwo amene akupita

m'nyumba ndi m'nyumba ndi kutenga akazi opusa - akazi opusa - otengedwa nazo zilakolako zamitundumitundu, osaphunzira kapena osakhoza konse kufika ku chizindikiritso cha Chowonadi." Sangakhoze...Sakanachita chimenecho, ndipo sangachite chimenecho. Mulungu anatero. Afarisi a khungu inu, simungawone chimenechi? Sindinakiye; Ndiku ngokhomerera msomali ndi kuwupindirira. Ngakhale mipingo sikhoza kuzindikira chimenechi. Akazi sangamvetse chimenecho; anayenera...Akazi opusa, otengedwa ndi zilakolako zamitundumitundu - Hollywood, zinthu za mitundu yonse, ometa tsitsi, obvala makabudula, odzola zodzoladzola ndi zopakapaka, zinthu za mtundu umenewu zimene ziri zosayenera.

<sup>166</sup> Kodi mukudziwa kuti mkazi akutenga mbali yayikuru m'masiku otsiriza? Kodi mukudziwa kuti Baibulo linati iwo amene adzathawamo mu chinyanso adzakhala nthambi yokongola pamaso pa Ambuye? Tsiku lina ndidzafika pa chimenecho, Ambuye akafuna, pakuti ndi - za inu akazi. Tangowanani chimene Mulungu akuganizira mkazi amene angathawedi chinyanso cha makono. Anati adzakhala wokongola.

<sup>167</sup> Ndinamumva mkazi akumuseka mtsikana tsiku lina - gulu la akazi ovala mwa pafupi kuvula, akazi makhalidwe onyansa - kuposa garu wamkazi - akuseka mkazi wokalamba wovala diresi lake lalitali. Mvetsetsani apa, akazi opotolozeka inu, iye ali ndi china chake chimene inu simukuchidziwa; ali ndi mkhalidwe. Kotero simudziwanso kuti dzina lake ndi chiyani. Zinatayika kale kwa inu. Simukudziwanso chabwino ndi choyipya; iye akudziwa. Ali ndi chinachake chimene chabisika mu mtima mwake chimene inu simukuchidziwa. Munachitaya; simudzachipezanso. Mukumutcha iye wa mbiri yakale, ndi zina zotero. chotero. Iye akudziwa china chake chimene inu simukuchidziwa. Ali nacho, chabisika mu mtima mwake chuma cha kudzilemekeza. Simukudziwa liwu limodzi la icho. Mayi anu amakulerani chotero. Abusa anu anachilola chimenecho; kuwonetsera pamene wayima. Ndikulalikira za iye pakati pano. Mukuwona? Mukuwona pamene mukupita? Mipingo...

<sup>168</sup> Yesu anati Malemo onsewa ayenera kukwani-ritsidwa; kotero akwaniritsidwa.

<sup>169</sup> Onetsetsani, monga Ayane ndi Ayambre anatsutsana naye Mose, adzadzanso...ena a iwo...Iye saku...Tsono, sakunena za a Methodist, a Baptist pano; ali kunja kwa malingaliro. Mukuona? Koma monga a Yane ndi a Yembre anatsutsana naye Mose ndi Aroni, koteronso, anthu osatsimikizidwa pa Chowonadi (opotolozekera ku miyambo ndi ziphunzitso za mipingo m'malo mwa Baibulo. Ndipo nthawiyo a Yane ndi a Yambre anakhoza kuchita chiri chose chomwe Mose akanachita. Mukuwona? Monga a Yambre (Mukuwona mmene



zikugwirizirana apo?) - monga Yane ndi Yambre anatsutsana ndi Mose, ndimomwe amachitira anthuwa osatsimikizi ka pa chowonadi namachikana sangakhale Nacho pa ubale wawo, sangathe ngakhale kugwirizana Nacho, alibe Nacho ntchito. Koma anati, “Kupusa kwawo kudzazindikirika.” Pamene Mkwatibwi ayima pa malo ake napita ku mwamba zidzaziwika, musadandaule. Monga Mose, pamene anatenga ana a Israeli ndi kuwaturutsa mu Iguputo, kotero Iguputo anamira. Chabwino.

<sup>170</sup> Yesu anati Lembo liri lonse analiuzira; kotero - kuti Lembo liri lonse liyenera kukwaniritsidwa. Pamene Iye...Iwo anali kufunsa, anati, “Ukudzipangitsa Wekha kukhala Mulungu.”

<sup>171</sup> Iye anati, “Inu m’chilamulo chanu munawatcha aneneriwo amene Mawu a Ambuye anadza kwa iwo, munawatcha milungu; ndipo mumalondola.” Anati, “Nanga mundiweruza bwanji Ine pamene ndinena kuti Ndine Mwana wa Mulungu?” Malembo onsewa amene auziridwa onse ayenera kusanduka thupi, onse ayenera kukwaniritsidwa. Mukuwona pamenepo, iwo anangokhala akhungu, anangotengeka ndi Mawu a anthu mmalo motengeka ndi Mawu a Mulungu. Ndi chimenecho chikuwapangitsa akazi kuchita zimenezo. Ndi chimenecho chikuwapangitsa alaliki kuchita zimenezo. Atengeka ndi bishopu m’ malo mwa Yesu. Atengeka m’menemo ndi - ndi thumba lawo la ndalama, khamu lalikuru.

<sup>172</sup> Tangowonani ngati ndiri wotchuka. Tatangani anthu a ku Jeffersonville, ndi kagulu kakang’ono kamene ndiri nako panoka kochokera mu Jeffersonville, tengani anthu a kunja amu Jeffersonville kunja kwa chihema chino m’ mawa uno, sindikanakhoza kukhala - kapena kukhala nawo theka la khumi ndi awiri oti ndiwalalikire. Ndi chiyani chimenechi? Iye wapangidwa kuchokera mu dziko monse, kuchokera ku New York mpaka ku Massachusetts, mpaka ku Boston, Maine, mpaka ku nyanja, Georgia, Alabama, ndi kuzungulira dziko lino. akusonkhana pamodzi. Amen! Ndi chiyani. . . Kudzakhala kuwala nthawi ya madzulo.

<sup>173</sup> Iwo sangazindikire Kuwala kwa nthawi ya madzulo; vuto lake ndi limenero. Sakutha kuzindikira. Ali ndi khungu lambiri. Baibulo linati ali otero.

<sup>174</sup> Russia anangolandira malo ake mu dziko la sayansi mosapitirira zaka pafupifupi makumi anayi zapitazo. Mukudziwa pamene nkhondo Yoyamba ya Dziko lonse inayambika, sanakhoze - sanasamalire za Russia. M’bale Roy, anangokhala chigulu cha anthu ozazindikira; Asiberia akulu akulu akale, a ndevu kumaso kwawo konse ndipo sanadziwe ku manja ndi kuti kapena ku manzere ndi kuti. Ndi zowona zimenezo. Russia. Koma anazindikira malo ake. Anayenera kuchita chimenecho pokwaniritsa Malembo. Mukudziwa mauneneri anga a chimene ndinanena kuti zidzachitika, m’mene

ena onsewo adzakhala mu chikominizimu. Tsono akutsogolera dziko lapansi mu sayansi. Ife tiri kutali kumbuyo kwake. Ena onse pa dziko lapansi ali pambuyo pake. Akutsogolera pa malo ake. Anangozindikira kuti anali ndi nzerunso.

<sup>175</sup> Onetsetsani. Munthu ali ndi ma sensi asanu ndi limodzi amene anali nawo mu zaka 6000 zapitazo. Kwapita zaka zikwi zisanu ndi chimodzi ali ndi ma sensi amene iye anali nawo azikhuzira nawo dziko la pansi namutumikira Mulungu. Koma tsopano mu zaka makhumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu zapitazo pamene munthu wachoka pa kavalo ndi ngolo nakhala woyenda mumlengalenga. Chifukwa chiyani? Anachoka pa chikhulupiriro chake pa Mulungu natembenukira ku zokhuzira zake ndi kukhoza kwake monga munthu. Munawonetsetsa chimenecho? Anachoka pomudalira Mulungu; amadzidalira yekha.

<sup>176</sup> Monga mkazi uyu wosakhulupirira Chikhristu (dzina lake ndi ndani?) ku Washington amene anasintho zonsezi? [Wina wake atchula dzina la mkaziyo - Mkonzi.] dzina lake ndi ndani? Murray. Iye anati, “Bola tiri ndi gulu la ankhondo a pamtunda ndi a pa madzi ndi mlengalenga; sitisowa Yehova wakale!” Ine sindisamala chimene tiri nacho, ndi Yehovah kapena opanda chirichonse. Magulu ankhondo ndi am’madzi zadzamira - ndipo adzatero, koma Yehova adzakhala wachikhalire. Ndipo ngati ndiri gawo Lake ndi Mwana wake ndidzakhala chikhalire ndi Iyeyo, osakhala mwa kuitana kwanga kapena kusankha kwanga, koma mwa kusankha kwake. Amen ndiponso Amen! Ndiribe kanthu kochitapo. Ndi Iyeyo. Mundipatse Iye kapena mundipatse imfa. Maiko akhazikitsidwe ndipo agwe; Yehova adzakhala chikhalire. Wachita chimenecho m’mibadwo yonse. Pamene Roma anagwa, pamene Iguputo anagwa, ndi ena onsewo anagwa; ndipo Iye wakhalabe Yehova. O, aleluya! Chipembezo chikundikomerano.

<sup>177</sup> Chifukwa chimene Russia anadzidziwa iye yekha, anayenera kutero. Monga m’mene Israeli anayenera kufika ku dziko lawo. Mulungu anayenera kuwafikitsa kwawo chifukwa cha Malipenga. Koteronso Mulungu anayenera kumufikitsa Russia kumeneko, mu chikominizimu, kuti achite chenichenicho chimene chinaneneredwa kuti adzachita.

<sup>178</sup> Munthu ndi zokhuzira zake asanu ndi limodzi wayenda ndi kavalo ndi ngolo yake, akudalira Mulungu. Mu zaka makuni asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu zapitazo anasiya zomudalira Mulungu. Pamene anasayina chikhazikitso cha boma lino la United States, anamuika Mulungu mu chiri chonse chimene anachita. Tsono sakusonkhananso, ndipo sakutchulananso Dzina Lake. Ndi choncho. Akudalira pa kutukuka kwawo mu sayansi, iwo - kuchenjera kwawo mu sayansi yawo. Gulu lodedeluka. Ndi zoono zedi. Dziko lonse lapansi lamezedwa mu umbuli wa Baibulo Dzi -

Dziko lapansi lapandukira Mulungu. Koma tangoganizani, mkatikati mwenimweni mwa zinthu zonsezo ndi mipingo ya zipembezo ndi zosayenera zawo zonse za ku seminary kwawo ndi zina zonse, Mulungu watenga Mawu a mneneri wake nadulamo Mkwatibwi...?..Iye anati adzachichita chimenecho. Wawadulamo mu zimenezo monga Iye analonjeza kuti adzatero.

<sup>179</sup> Akudalira pa nzeru zawo, sayansi yawo ndi zina zotero, amusiya Mulungu, amene anamudalira nthawi ina. United States wasiya Mulungu. Anamuchotsanso ngakhale mu sukulu, ana athu aang'ono sangakhoze kumvanso za Iye. Amuchotsa mu sukulu. Tsono, akuyetsetsa kumuchotsa Iye pa ndalama ya dollar. "Tikudalira mwa Mulungu." Akudzachotsa ulemu yawo pa mbendera. Fuko Limodzi pansi pa Mulungu; adzathetsa zimenezo.

<sup>180</sup> Mukuona, apita ku zilingaliro zao ndi maganizo awo. Chifukwa mu zaka makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu zapitazo sanasinthe mpang'ono pomwe mu ma sensi ake, ndi munthu yemweyemweyo amene Mulungu anamulenga pa chiyambi. Koma mmasiku otsiriza ano, kodi simungakhoze kuzindikira pamene tiri? Mpingo wachoka pa Mulungu kufuna chimenecho, ku seminare, ndi kujayira ndi zina zoterozo, mmalo mwa Mawu. Sakumuzindikiranso Iye mu misonkhano yawo, m'masukulu awo, kapena palibenso za Iye.

<sup>181</sup> Israeli pa zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu zapitazo wazindikira kuti china chake chawabweretsa ku dziko lakwawo monga mwa lonjezano. Sakudziwa m'mene zinachitikira. Anavutika monga china chiri chonse, kuphedwa mu nthawi ya Malipengayo; komano ali mu dziko lawo. Sakudziwa chifukwa chake.

<sup>182</sup> Chifukwa chiyani Rasha anadzuka? Chifukwa chiyani maiko anadzuka? Ndi chifukwa chiyani anthu akhoza kutukuka, pamene anthu a sayansi pa zaka mazana atatu zapitazo... Munthu wina wa chi Fransa wa sayansi anagubuduza mpira pa dziko pa liwiro lina lake ndipo anatsimikizira ndi kufufuza kwa sayansi kuti ngati munthu athamanga liwiro lowopsya la mitunda makumi atatu pa ora limodzi, mphamvuya kukoka kwa pansi ikhoza kumuchotsa pa nthaka, malinga ndi kulemera kwake, malinga ndi kulemera kwa mpira. Tsono akupita pa mitunda zikwi khumi ndi mphambu zisanu ndi ziwiri pa ora limodzi, kumangoonjezerabe. Angotulukira zimenezo posachedwapa. Chifukwa chiyani? Ziyenera kukhala momwemo.

<sup>183</sup> Chifukwa, mpingo unali - unayima pa tanthwe la Yesu Khristu. Zinalibe kanthu zimene wina anganene, anangokhala ndi Mawu omwewo, uthenga wa nthawiyo, Luther, Wesley,

kupita m'musimo. Kotero tsopano, abwereranso ku miyambo. Chifukwa chiyani achita zimenezo?

<sup>184</sup> Zaka mukumi awiri ndi mphambu zisanu zapitazo, Israeli wangozindikira kuti ali ku dziko la kwawo pa china chake. Chinaneneredwa kuti adzasonkhanitsidwanso; Hoseya anatero. Tikhala-tawerenga pa kanthawi kapitako. Mulungu atithandize kuchimvetsa. Chabwino.

<sup>185</sup> Nthawi yomweyonso Mkwatibwi wazindikira Kuwala kwa nthawi ya madzulo, wangoyamba kuzindikira. Achipentekoste anjala ayamba kuzindikira kuti mabungwewo alibe chimene iwo akuchifunafuna. Angopotolozoka ndi kung'ambika. Mukuona ndi nthawi ya kuzindikira, kuzindikira. Muyenera kuzindikira. Dziko lazindikira. Mayiko azindikira. Sayansi yazindikira. Mdierekezi wazindikira; ndi nthawi yoti akhoza kuwononga azimayi, kuononga mpingo, kuononga anthu. Wachizindikira chimenecho. Kotero Mulungu wazindikira kuti pali anthu pa dziko lapansi amene Iye anawasankhiratu ku Moyo. Iye wazindikira kuti ino ndiyo nthawi yotumiza Uthenga Wake; Iye anachita chimenecho. Anthuwo achizindikira chimenecho. Mkwatibwi wazindikira Kuwala kwa nthawi ya madzulo.

<sup>186</sup> Ngati Sodomu akanangozindikira tsiku lake pamene anawaona atumiki aja akudza kumeneko, monga Billy Graham ndi Oral Roberts. . .

<sup>187</sup> Tsono, anthu ena odedeluka ku Pheonix anangoyamba kumene - anangotsegula mbali yokhayo pa - tepi nanena. . . Ndinati pano, "Ndiyenera kubatizidwa mu Dzina la Yesu," ndinatero. Kotero anati, "Tsono, mukuona papa, apa anati. . ." pamene ndinali kulankhula za ku Afrika, m'mene amabatizira katatu akuyang'ana pansu ndi kubwerera. . . Anati ndinati, "Sizikusiyana." Mukuona, sanamvere tepi yonseyo, kagawo kokha basi ndikutseka chimene chiri mulandu waukulu kuchita chimenecho; Matepi amenewo ali ndi chilolezo chonse cha boma. Palibe wina amene angasewere nawo. Musayesere kutero. Ngati mutero, boma liri pa inu. Koma tingachite chimenecho? Ayi Iye anati, "Asiyeni okha," Mulungu anandifotokozera chimene chidzachitika. Muzingoyang'anitsitsa, mungoyang'anitsitsa diso lanu pa munthu ameneyo. Mukuwona?

<sup>188</sup> Nthawi yomweyomweyo Mkwatibwi wazindikira Kuwala kwa nthawi ya madzulo. Sodomu akanangozindikira ora lawo. . .

<sup>189</sup> Tsono, munthu yemweyemweyo anaika pa tepi, anati "Tawonani, kwa inu anthu a Pentekositi," anati, "Ndi inu a Baptist: Munthu uyu, mneneri wonyenga, William Branham (Mukuwona?), wanena kuti Oral Roberts ndi Billy Graham anali mu Sodomu." Mukuwona? Kotero anadula tepiyo. Ndi zokhazo. Mukuwona? Sanakhoze kupitiriza kunena kuti anali atumiki a ku Sodomu. Osati mu Sodomu; koma iwo ali kumeneko

monga mtumiki ku Sodomu. Aliyense akudziwa kuti ndinanena choncho. Mverani tepi yanu. Aliyense amene adzachotsera kapena kuonjezerapo, chimodzimodzi chidzachotsedwa kwa Iye. Mukuwona? Ngati ali Mawu a Ambuye, adzaima momwemo.

<sup>190</sup> “Sodomo akanangozindikira atumiki ake, akanakhala alipobe lero,” Yesu anatero. Akanangozindikira monga momwe Abrahamu anazindikira... Abrahamu anadziwa kuti pali mwana wamwamuna wolonjezedwa akudza. Koma anadziwa kuti payenera kukhala kusintha kwa njira ina, chifukwa anali wokalamba kwambiri chimodzimodzinso Sarah. Koma pamene anamuona Iye Uja amene anakhoza kudziwa maganizo a Sarah amene anali kumbuyo kwake, anazindikira nthawi imene iye anali kukhalamo, kotero anati, “MBUYE Wanga, ndi loleni nditenge madzi pang’ono apa nditsuke mapazi Anu.” Anadya ka mkate. “Ndi kupempheni Inu, mukhalebe kwa kanthawi kena.” Mukuwona? “Pano M-B-U-Y-E wanga (zilembo zazikulu M-B-U-Y-E, Elohim).” Anazindikira kuti Mulungu anali kulankhula naye mu thupi la munthu. Anazindikira chizindikiro chake, ndipo anadalitsidwa ndi MBUYE. Sodumu sanazindikire tsiku lawo ndipo anawochedwa. Yesu anati, “Monga zinakhaira mu tsiku limenelo, koteronso zidzakhala pamene Mwana wa Mulungu a - kapena Mwana wa munthu adzawonetseredwa.”

<sup>191</sup> Tsono, mpingo sunazindikire tsiku lake. Monga Israeli anaumirizidwa kubwerera ku Palestina, udzaumirizidwa kulowa mu Bungwe la mipingo yonse mziko lapansi (WCC). Chifukwa chiyani? Sanazindikire Ora lake. Turukanimoni anthunu! Musakhale ophatikizana nawo matchimo ake! Thawitsani moyo wanu, kapena mudzagwidwa ndi chizindikiro cha chirombo, ndipo simudzachitapo kanthu. Iye amene ali woyipa akhalebe chiyipire. Iye amene ali woyera, osati adzakhala woyera - woyera tsopano... Iye amene ali woyera, osakhala mkazi wometa tsitsi; sangakhale. Tsono zimene ndi zomveka mvemvemve, koma ndi Malembo amenewo. Baibulo limanena kuti amanyoza mutu wake. Ndipo mutu wake ndi mwamuna wake. Mutu wa mwamuna ndi Khristu; kotero amanyoza Khristu. Akhoza bwanji kukhala wonyozetsa ndi kusakhala woyipa? Iye amene ali wometedwa akhalebe chomwecho! Iye amene - mkazi amene amasunga - wovala makabudula azivalabe! Iye amene akukana Mawu adzikanabe! Koma iye amene ali woyera akhalabe woyera! Iye amene ali wolungama akhalebe chilungamire, Mawu olungama a Mulungu, Mwana wa Mulungu wowonetseredwa. Mukhalebe woyera, olungamabe, Muzindikire. Inde, bwana!

<sup>192</sup> Masiku... osati... Mpingo sunazindikire tsiku lake, monga Israeli amene wabwerera ku dziko lake lalonjezo. Sakudziwa m’mene anafikira kumeneko. Anangopezedwa atabwezeretsedwa kumeneko. Chifukwa chiyani? Mphamvu ya mayiko inamukhazikitsa pa malo pake. Tsono, ndinenapo china

chake. Mphamvu ya mayiko inayika Israeli mu dziko mwake. Mphamvu ya mayiko idzayika mpingo mu Bungwe la Mipingo yonse mdziko lapansi. Koma Mphamvu ya Mulungu idzayika anthu mu Mkwatibwi. Mphamvu za dziko zikukanikizira mbali iyi, ndi mbali iyo, koma Mulungu akukokera m'mwamba, Mzimu wa Mulungu, umene uli Mawu a Mulungu. (Mawu anga ndi Mzimu ndi Moyo ndipo adzayika Mkwatibwi m'malo mwake, chifukwa adzazindikira malo ake mu Mawu; kotero ali mwa Khristu.) adzamuyika iye m'malo mwake, Palibe mphamvu ya dziko imene idzachita chimenecho. Koma mphamvu ya mayiko inapititsa Israeli ku dziko lake. Mphamvu ya Bungwe la mipingo pa dziko lonse idzakankhira gulu liri lonse m'menemo, koma Mphamvu ya Mulungu idzakweza Mkwatibwi ku Ulemerero, kuchoka mu chimenecho.

<sup>193</sup> O, anthu, zindikirani tsiku lanu, monga Yesu anakuchenjezani inu, chizindikiro cha sodomu, ndipo mkhalidwe wa mpingo tsiku lino.

<sup>194</sup> Taonani chimene Ananena kuti chidzachitika mu tsiku lino. Mumvetsere kwambiri. Chizindikiro cha Sodomu chidzachitika mu tsiku, chizindikiro monga Abrahamu tsiku lija amene anaturutsidwa asanafike Sodomu. Zinthu zonse izi zimene zinaneneredwa zizichitika tsopano lino. Yang'anitsitsani tsiku limene mukukhalamo. Tabwerezabwerezwa.

<sup>195</sup> Tsono, analonjeza kukutumizirani Kuwala kwa ku Mwamba kudzakhwimitsa Mbewu ya Mawu imene idzafesedwera tsiku ili. Mbeuyo ili muno. Mbewuyo ndi Baibulo. Chifukwa chiyani? Yesu anatero: Mawu ndiwo Mbewu imene Wofesa afesa. Kotero tsono, musanakhale ndi m'mera uli wonse, ziribe kanthu mukafesa mbewu iyenera kukhala ndi kuwala kuti kukhwimitse mbewu imeneyo, kapena ayi idzavunda ndipo sidzachita chabwino chiri chonse; idzawonongeka. Koma ngati mbewu ili pansu, malo oyenera ndi kuwala koyenera mmenemo, iyenera kukhwina. Kotero Iye analonjeza chimenecho m'masiku otsiriza mu nthawi ya madzulo Dzuwa lidzadza kudzakhwimitsa Mbewu imeneyo. Mbewuyo ikulalikidwano. Mwana wa Mulungu akakhwimitsa Mbewu imeneyo pakuitsimikizira, kuipangitsa Iyo kuturuka pamaso panu, ndikutsimikizira kuti ndi zolondola. Kodi mukuchigwira chimenechi. Zindikirani tsiku lanu.

<sup>196</sup> Ndipo Laodikaya wolemera, wakhungu, wophunzira adzachotsa Mawu pakati pake. Kodi achita chimenecho? Iye anati adzatero. Monga aneneri akale anatumizidwa kukatsimikizira Mawu olonjezedwa a mu tsiku lawo, kotero kuti anthu amene anadziwiridwatu mu tsiku lawo anawona, monga mkazi wa pa chitsime, monga Natani, monga Batureyo, monga Petro, ndi ena onsewo amene anachizindikira... Iye anali Mawuwo ndi chopezekapocho. "Ngati Ine sindichita ntchito zimene Atate wanga analonjeza kuti ndichite, kotero musandikhulupirire Ine. Koma ngati ndichita

ntchitozo, angakhale simukundikhulupirira Ine khulupirirani ntchitozo; zikukufotokozerani za Ine.” Mwamvetsa? Chabwino. Osaliphonya tsikuli. Anatomiza. . . Amuna ndi akazi a masiku ena anachizindikira, nalowamo, ndipo anatetezedwa.

<sup>197</sup> Inu Apentekosite (O, kalanga ine!) chifukwa chiyani simuzidikira tsiku lanu? Zindikirani tsiku la nthawi ya madzulo. Iyo ili pano, ili pano ku - kutsimikizira kubwera kwa Khristu, kutsimikizira ilo. Tiri kumapeto. Zindikira tsiku lako.

<sup>198</sup> Ndikudziwa ndakusungani nthawi yaitali. Ndi 12 kololo tsopano. Koma ndimakonda chakudya chimenechi. Umenewu ndi Moyo; ndi - ndi cha kwa okhulupirira. Zindikirani tsiku limene inu mukukhalamo ndi chizindikiro cha nthawiyo.

<sup>199</sup> Tawonani pamene zonse zikupita, Israeli; pamene mpingo, pamene ochita zosayenera pamene Mkwatibwi akuyima. Chatsala ndi chiyani; chinthu chotsatira? Kutengedwa kwa Mkwatibwi. Chifukwa, mpingo uli wonse ukuyang’anira chinthu chachikuruchi. A Pentekosite akuti, “Ulemerero kwa Mulungu! Padzafika tsiku limene iwo ati adzachite ichi ndipo adzachita icho.” Mukuwona, ndi ongolankhula. Amakhulupirira.

<sup>200</sup> Monga nthawi ina Kayafa anati, “Kodi sikuli koyenera kuti munthu m’modzi afe ndi kuti usawonongeke mtundu wonse?” Iye Anali mkulu wa ansembe, Baibulo linanena, chifukwa chimene analankhulira chimenecho. Ananenera, asakudziwa chimene akulankhula. Koma anazindikira kodi choonadi chenicheni cha chimenecho, kuti anali kumpereka Mulungu yemweyo amene iye amadzinenera kuti anali wansembe wake? Koteronso ziri chomwecho lero! Akuyang’ana uko kwina kwake kuti - nthawi yopambana ifike.

<sup>201</sup> Chifukwa chake, ndimapita m’misonkhano ya anthu malonda ndi ena, iwo amati, “Ulemerero kwa Mulungu!” Alalikiwo amangoyima kuchikolezera chiguluchu, ndi kunena “Kukudza chitsitsimutso chopambana. Dzanja la? Ambuye lidzakhala pa dziko lapansi!” Ndipo m’mene anthu akupitira, kuthamanga ngati. . . Ndipo osazindikira kuti zimenezo ziri mu Malipenga a Israeli. Chifukwa chiyani akuchita chimenecho? Ndi chifukwa chakuti ndi ongozitchula Akhristu, ndipo sazindikira. Ngakhale Kayafa sanazindikire chimene anali kuchita. Koterom sakuzindikira kuti akukana Uthenga womwewo umene watumizidwa kwa iwo. Amen!

<sup>202</sup> Mbali iliyonse ya Malembo tapitamo tsiku ndi tsiku ndipo sabata ndi sabata, mpaka chakhala Chowonadi chosakhoza kuchitsutsa, “Ngati akhungu sangachilandire Chimenechi,” Yesu anati “Muwaleke okha. Ngati wakhungu atsogolera wakhungu mzake onse adzagwa m’mbuna. Sindikudziwa ndi liti; sindikudziwa ndi kuti; koma ndikudziwa kuti zirikudza.

<sup>203</sup> Mukudziwa, ndikuwona chifukwa chimene Satana sanafune kuti ndichite chimenechi. Dzulo sindinali kupeza

bwino. Sindinakoze kupeza Liwu kuchokera kwa Ambuye. Ndinachita chirichonse chimene ndinadziwa kuchichita, ndipo sindinakoze... Ndipo m'mawa uno pamene ndinadzuka... ndinadya - chimanga dzulo, ndipo kungokhala ngati changokhala m'mimba momwemo. Ndinadwala kwambiri ndinango - sindinakoze kudzuka. Ndinaganiza, "Chikuchitika ndi chiyani? Ndikupita kunja, ndipo sindikudziwa chimene ndingakalankhule. Ndipo Ambuye, sindikukhoza kupeza Lembo m'mutu mwanga loti ndilembe; sindikupeza chirichonse." Sindikukhoza kudziwa choti ndichite. Koteru pamene uthenga unayamba kudza kwa ine, Satana anali kumangoti "sukupeza bwino. Mutu wako ukupweteka. Ukudwala. Sungapite kumenekuja. Sungathe kuyima. Zikhala motere, zikhala motero."

<sup>204</sup> Ndikukumbukira nthano ya munthu wosapenya bwino ku England. Iye anangokhala munthu wamba. Ndipo ananena kuti m - m - mfumu, mmodzi wa mafumu m'masiku akalewo anali kupita mu - m'nyumba mwake. Ndipo uyu... Analibe wina aliyense... Anali ndi uthenga umene anayenera kutumiza, wofulumira, chifukwa mdani... Koteru iye - Iye anati kwa munthu amene anayima pamenepoyo, anati, "Pano, tenga uthenga uwu, tenga uthenga uwu! Fulumira upite ku malo akuti, akuti, ndi kulamulira ichi chichitike." Ndipo anati, "Tenga ndodo yanga mdzanja lako; idzakutsi-mikizira iwe, kuti ndine - watumidwa kuchokera kwa ine."

<sup>205</sup> Ndipo anayika iyo mu chobvala chake, namuka, alonda paliponse akumuimitsa iye wina aliyense, akufuula, "Ndipatseni njira! Ndiri ndi uthenga wa mfumu. Ndine mthenga wa mfumu!" Mawu otsimikiziridwa!

<sup>206</sup> Ndinaganiza, "Satana, choka pa njira yanga! Ndiri ndi uthenga wa Mfumu. Ndiyenera kupita!"

<sup>207</sup> Nthawi ina pamene anamupha Kalonga wa Mtendere, ndi kumuyika Iye m'manda, ndi kutsekera mandawo, ndipo imfa inamugwira iye masiku atatu ndi usiku utatu, koma pa m'mawa wa Kuwuka kwake Iye anali ndi ndodoyo m'dzanja Lake ndipo anafuula! "Choka imfa! Choka manda! Tseguka! Ndine Uthenga wa Mfumu. Ndiyenera kuturuka kutsimikizira chiukitsiro chimenechi. Ndine kuuka ndi moyo!' Aleluya! Ndikungomva bwino kwenikweni tsopano. Ndi uthenga wa Mfumu. Tiyeni tizindikire chimenechi, abwenzi, pakuti tayitanidwa kusonkhana pamodzi kusonkhanira kulira kwa Lipenga. Pakuti Lipenga la Ambuye lidzalira ndipo sikudzakhalanso nthawi.

<sup>208</sup> Wasonkhanitsa Israeli. Masiku atatuwo-pa tsiku lachitatu Iye anati adzachita chimenecho. Zaka mazana makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi ziwiri zapita. Mu tsiku lachitatu limenelo Iye anati adzawasonkhanitsa iwo pamodzi, ndipo wachichita



chimenecho. Iye anati adzazindikiritsa njira ya Moyo. Ndi amenewo ali kumeneko, kungoyembekezera Mkwatibwi achoke panjira kotero akhoza kubwera aneneri awiriwo, aneneri a chi Heberi, amene adzazindikira.

<sup>209</sup> Mukukumbukira ine nditaima mu Cairo, popita kumeneko, pamene Lewi Pethrus anati, “M’bale Branham, ngati angaone chimenecho. . . Iwo amakhulupirira aneneri.”

<sup>210</sup> Ndinati, “Ndi chinthu chabwino kwa ine.” Mukuwona m’mene munthu ali? Koma tawonani chisomo cha Mulungu? Ndinati, “Ndiwerenga Chipangano Chatsopano ichi.” Iwo amachiwerenga. Lewi anawatumizira kumeneko oposa miliyoni, M’bale Lewi Pethrus wa ku Sweden. Akuchiwerenga ayamba kubwerera kumeneko Iwo Ayudawo - Osati monga gulu la Ayuda amakonowa, koma ku dziko la kwao. . . Abwera nanena, “Ngati uyu ali Mesiya, tiyeni timuwone Iye akuchita chizindikiro cha mneneri, tidzakhulupirira.”

<sup>211</sup> Lewi Pethrus anati, “M’bale Branham, pali mwayi pamenepo, pali mwayi pamenepo! Winawake anandiuza kuti padzakhala mwayi. Ndiri ndi choyendera,” anati, “mpaka kumeneko.” Munthu wina anadza nakhala pamenepo ndi Mbale Argenbright, anati, “M’bale Branham, chimenecho chidzangochenjeza Israeli! Mukawawonetse chimenecho ndi kuwawonetsa chizindikiro cha mneneri, iwo adzakhulupirira.”

<sup>212</sup> Ndinati, “Ambuye, pano ndiri wokonzeka.” Ndinathamangira ku ndege (kutenga ndalama ndikugula tiketi): ndinayima mu Cairo; ndinati “Inde, ndiri wokonzeka.”

<sup>213</sup> Mzimu Woyera anati, “Awa si malo ako. Ino si nthawi yako.” Mukuona? Umathamangira za mtsogolo. Ndinaganiza “O mai, ndabwera konseku mpaka kuno, ndipo ine ndikupita.”

<sup>214</sup> Chinachake chinati, “Ima pomwe pano! Usapite njira imeneyo. Tembenukira ku India. Usapite uko. . . Pita ku India, koma usapite kumeneko!”

<sup>215</sup> Ndinaganiza, “Chifukwa chiyani zi. . .” Ndinatuluka kunja kwa bwalo la ndege ndinati “Ambuye Yesu, chikutanthauza chiyani chimenechi?” Ndiye Iye anandizindikiritsa. Pokhala wa Amitundu. . . Aneneri amenewa ndi amene adzachite, ziyenera kukhala molingana ndi Malembo. Mose ndi eliya ayenera kudza. Ndipo kuwonjeza pa chimenecho, Mkwatibwi sanachotsedwe padziko. Ndipo aneneriwo adzabwerera, ndipo adzachita chizindikiro cha m’neneri. Amenewo ndiwo Malembo. Pamenepo zonseno zikwaniritsidwa mwa ngwiro. Israeli monga mtundu adzabadwa tsiku limodzi. Amen! Nyali za Madzulo zikuwala.

Kudzakhala kuwala nthawi yamadzulo  
Njira ya ulemerero mudzaipezadi;

Munjira ya madzi muli kuwala lero  
 Kubatizidwa mu Dzina lopambana la Yesu.  
 Ana ndi akulu, lapani machimo anu onse,  
 Mzimu Woyera udzalowa mwa inu zedi.  
 Kuwala kwa madzulo kwabwera.  
 Ndi zowona kuti Mulungu ndi Khristu ndi  
 m'modzi.

<sup>216</sup> Tiri mu nthawi yotsiriza, abwenzi. Ndipo kotero tikuganizira za nyimbo ya wolembe wowuziridwa ndi Mzimu pamene anati:

Mafuko akuphwasuka; (Izi ndi pafupifupi zaka khumi ndi zisanu zapitazo.) Israeli akudzuka;

Zizindikiro zoloseredwa ndi aneneri;  
 Masiku a Amitundu atha (Taonani zonyansa zao tsopano) Zowopsa zikuchuluka.

Bwererani, omwazika, kwanu.

Tsiku lachiwombolo layandikira;  
 Mitima ya amuna ikuyima ndi mantha.  
 Zazidwani ndi Mzimu wa Mulungu, Nyali zanu zitayeretsedwa ziwale.

Yang'anani mwamba! Chiwombolo chanu chayandikira. (Ndi momweno)

Aneneri abodza akunama; Chowonadi cha Mulungu akuchikana; (Kodi chimenechi si choonadi!)

Kuti Yesu khristu ndi Mulungu wathu. (sakukhulupirira chimenecho. Ali ndi mitundu yonse ya ma "ism" ndi zinthu...?...koma mneneri anati - kapena wolembe wozodzedwayu anati)

Tidzayenda momwe atumwi anayenda.

<sup>217</sup> Mukukumbukira masomphenya anga? Ndinati, "Ngati anthu a Paulo akalowa, koteronso anga, chifukwa ndachita momwemo monga iye"...?...Ndipo mamiliyoni anakweza manja awo, ndikunena, "Tikudalira pamenepo!" Chiyani? Zindikirani tsiku limene tikukhalamo, nthawi imene tikukhalamo, chizindikiro cha nthawi imene tikukhalamo. Zikhoza kukhala kuti nthawi yatha kusiyana m'ene tikuganizira. Limodzi mwa masiku akudzawa iye amene ali kunja akhalebe kunja. Iye amene ali mkati akhalebe mkati momwemo. Chitseko chidzatsekeka.

<sup>218</sup> Ngati pali ena pano m'mawa uno amene sanayendemobe, O, mu Dzina la Yesu, anthu anga okonedwa, musayang'ane wantchito wosaphunzira wayima panoyu, wosatha kuwerenga, wosaphunzira, wosaphunzira - musayang'ane chimenecho, koma muyang'ane Mawu amene akutsimikiziridwa. Tayang'anani Mzimu Woyera Amene akuwatsimikizira kuti ndi

Choonadi. Tiri mu nthawi ya madzulo. Nthawi yatha kusiyana ndi m'mene mukuganizira . . . Musa . . .

219 Akazi, siyani tsitsi lanu likule. Mlongo, chonde chotsani zovala zosayenerazo. Tayani nduduzo. Pakuti ora lidzafika pamene Iye amene ali woyipa, akhale chiyipire, ndipo iye amene ali wolungama akhale chilungamire. Iye amene alowa mkati akhala mkati; iye amene ali kunja akhala kunja. Malire ochepa apafupi ngati kuli kovuta kuti wolungama akapulumsidwe, nanga wochimwa ndi opanda Mulungu (okana - choonadi, mukudziwa), adzayima pati? Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

220 Tsono, mu Kuwala kwa nthawi ino imene ife tikukhalamo, Kuwala kwa mu tsiku limene ife tikukhalamo tsopano, opambana ndi okonedwa, inu amene mukuchokera mu mayiko osiyanasiyana mu dziko muno, tiyeni tsono, ndi ine pamodzi ndi inu pa guwa pano, tiyeni titenge mndandanda. Kodi Mzimu wa Mulungu uli bwanji m'mitima yathu lero? Kumbukirani, ndi Mzimu umenewo, wosatsu-tsidwa, wosayipitsidwa . . . Chiphunzitso cha mpingo chiri chonse ndi zina zonse zapitiratu.

221 Osayesera dala kuwonjeza kapena kuchotsera pa chimenecho. Pakuti mukayesa kuika tanthauzo inu nokha, gawo lanu lidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo. Kodi mukuyesa kulankhula china chake chimene Mzimu sanalankhule? Kodi mukuyesa kuchipangitsa kuti Chimveke ngati chanena china chake, kapena mukungotenga chomwecho chimene chanenedwa ndi kuchisiya momwemo? Kodi mukulekanisa, mukudula, kugogoda, kuchita zinthu zimene siziri zabwino? Inu mwachita . . .

222 Mukuti, "Chabwino, sindikumva ngati ndingachite chimenechi kapena ine . . . Ine - Ndikudziwa mpingo wanga sukukhulupirira zimenezi. Angokhala mawu a munthu m'modzi pa chimenechi." Munthu m'modzi ameneyo ndi Mulungu. Baibulo ili pano limati musamete tsitsi lanu. Awa . . . Baibulo linanena kuti zidzachitika kuti akazi adzavala zovala ngati mwamuna, ndi m'mene adzakhalire chonyansa kwa Mulungu. M'mene Mzimu Woyera analankhulira mwa icho, chodzichepetsa, chotengeramo chosayenera ichi chimene changopezeka mu m'badwo umene Mfumu Yopambana inati, "Pano pali manda Anga Mawu Anga - Pano pali ndodo Yanga, makamaka. Tenga Ndodo Yanga, nupite nukapereke Uthenga."

223 Ndikudziwa zipembedzo zinayesetsa kuuimitsa, kuwukana, kunthamangitsira kunja, ndi kuumenyera kunja, ndi zina zonse; koma mwa chisomo cha Mulungu ndiri pa njiri yanga, kufuula ku fuko ndi fuko, ku malo ndi ku malo, ku mpingo ndi ku mpingo, "Turukani m'menemo!" Ndi zosatchuka, koma ndi Choonadi.

224 Kodi mungazilandire mwa - mwa - mwa Mzimu momwe zinalembedwera? Kodi mungazilandire mwa Mzimu momwe zinaperekedwera? Ngati munali musanatero, ife - palibe malo

a guwa (Mtima wanu ndiwo guwa), kodi mungakweze dzanja lanu, ndikunena, “Mulungu, mundichitire chifundo ine. Lolani Mzimu wa Mulungu udze mwa ine, kunditsutsa tsono za machimo anga onse ndi zokhumudwitsa, zikhalidwe zanga zonse zoyipa; ndi kupsa mtima, makangano, kumenyana, ndi kulimbana ndi zina zonse zimene ndakhala ndiri nazo. Ndipo ndikudziwa china chake kuti mzimu wanga suli wofewera ku Mwamba. Mundifewetse ine, Ambuye, mu mphindi yotsiriza iyi. Mwina uno ndi ulaliki wotsiriza kuwumva. Mwina ino ndi nthawi yotsiriza kuwumva Uthengawu. Ndakweza dzanja langa. Mulungu, mundichitire chifundo.”

<sup>225</sup> Mulungu akudalitseni. Manja madazeni. Tsono, mwa kamphindi pang’ono kopemphera mwa kachetechete. Inu amene munakweza manja anu, mukuonesa kuti muli okondweretsedwabe. Zikuoneka kwa ine ngati Mzimu akuitanabe winawake.

<sup>226</sup> Mulungu wokonedwa, Inu Amene mumadziwa zinthu zonse. Ndipo munapanga. Zinthu zonse pa cholinga cha zinthu zonse. Pakuti ena anayenera kutsutsidwa; ena anayenera kuchititsidwa khungu; ena, monga woumba mbiya anaumba chotengeramo, monga Paulo ananena, china chaulemu ndi chinacho chopanda ulemu. Chimene chinapangidwa chopanda ulemu chinali chongokhala kuti chikawonetsera icho chimene chiri chaulemucho. Koma siziri kodi m’manja mwa Woumbayo kuchita chimene Iye akufuna? Siziri kodi mu pulani ya kudziwiratu kwa Mulungu poitana... Iwo amene anawadziwiratu anawaitana, Iwo amene Iye anawaitana, anawalungamitsa. Ndipo iwo amene Iye anawalungamitsa anawapatsa ulemerero.

<sup>227</sup> Mwina ena a iwo pano lero ali ngati kamkazi kaja ka pa chitsime, kotayika mu zonyansa, kotayika mu miyambo ya anthu, kotayika mu ziphunzitso zopangidwa ndi anthu. Mwina mwake ndi koyamba kumva zinthu zimenezo, koma china chake chachenjeza mitima yao mwa chilendo. Pali manja ambirimbiri amene akwezedwa, Ambuye, Lolani Woumba mbiya wopambana atenge chotengeramocho tsopano nachiumbe kuti chikhale chotengeramo cha ulemu. Ndikhulupirira pali chifukwa, Ambuye, kapena sakanakhoza kuchita chimenecho; sakanakhala akunena chimenecho. Ndikhulupirirabe, powathandizira iwo.

<sup>228</sup> Lolani kapolo Wanu wodzichepetsa awathandizire, Ambuye. Tiloleni tiwathandizire iwo monga wina amene akuima pakati pa amoyo ndi akufa, monga wina mu Sodomu anali kuwatetezera a ku Sodomu, “Turukanimo, turukanimo msanga!”

<sup>229</sup> Atabwera Ambuye, mozichepetsa ndi mokoma ku mpando wachifumu wa Mulungu tsopano m’mitima yao, ndikunena, “Yesu, kuyambira lero mpaka mtsogolomu mudzakhala

wanga. Ndikuchita lonjezano limeneli kwa Inu tsopano pamene ndakhala pano pamene Mzimu Wanu wandikhuza. Ngati wandikhuza pano, sindingapitenso patali poposa pano. Pomwepano ndi pamene Inu mwandipeza; pomwepano ndi pamene zonse ziti zithere, pomwepano pa mpando wachiwiri, mpando wachitatu, mpando wachisanu, paliponse pano. Pomwepano ndi pamene chikakhazitsidwe, chifukwa ndi pano pamene mwanditsutsa; ndipo pano ndi pamene mwandilonjeza kuchikonza. Pakuti ngakhale ndinganyanse ndi kuyipa, ndiyeretsedwa ngati matalala. Ndikukhulupirira Mawu Anu onse; ndiri wokonzeka kuyenda m'menemo, kuwakhulupirira, kuwalandira. Ndipo tsopano ndikuchita ichi mwa ulemelero kwa Mulungu, kudziwa kuti moyo wanga suli wabwino kwa ine, suli wabwino kwa Mulungu, suli wabwino kwa anansi anga, suli wabwino kwa chinachirichonse koma kungoti-wabwino kwa mdierokezi pondipanga - kachitsiru kake, kumangondizunguza, mwina kukhala chidole cha mwamuna wina kuti azichiyang'ana, kapena kukhala chidole cha mkazi wina. Koma Mulungu, mundipange ine kapolo Wanu. Tipatseni, Ambuye." Ndikuwapereka iwo kwa Inu mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ndi mitu yathu yoweramitsidwa ndi mitima yathu:

Ndimva mpulumutsi wanga akuyitana,  
(Moona abwenzi, ikhoza kukhala nthawi  
yanu yomaliza. Kodi mukhoza kumva liwu  
laling'onolo?) akuyitana,

Ndi (Ndi chiani Iye. . . Ndi chiani chikuitana  
inu ngati Mphulumutsi wanu? Mau.)  
Mpulumutsi akuyitani (Ayenera kuchita  
chiani? Kukana za dziko ndi. . .)

"Tenga mtanda wanga nditsate, nditsate,  
(Ndanyozera ubatizo mu Dzina la Yesu,  
Ambuye.)"

Ndidzapita Naye m'mundamo,  
Ndipita (Ndi Iye kuti? M'madzi, mmunda,  
kulikonse, nyumba ya mapemphero, mu  
dziwe, kulikonse, Ganizirani.)

. . . pita naye. . . pita Naye mmundamo,  
Ndidzapita Naye, Naye konseko.

Ndizanka Naye mchiweruzo,  
(Ngati Mawu ali okhoza kapena mpingo ndi  
wokhoza)  
Ndipita. . .

"Ngati ndiri wokhoza kapena Iye wokhoza. Kodi chikumbumtima changa ndi chokhoza kapena Mawu Ake ndiokhoza?" Muli pa malo a chiweruziro tsopano. "Chimene ndakhulupirira, ndi chokhoza, kapena Mawu Ake ndi okhoza?"

Kodi ndikunganiza kuti ndi chokhoza kukhala ndi tsitsi laling'ono ndi kuvala makabudula? Kodi ndikuganiza kuti ndi zabwino kukhala wa chipembezo?" Iye ananena chiyani?)

Ndidzapita Naye, Naye konseko.

Tsopano komwe Anditsogolera ndidzatsata,

Ndakwezanso manja anga, Ambuye. Ambuye, khaya ndi kuti, uthenga wotsatira ukalalikidwa kuti? Kodi ndi panonso usiku uno? Ku Afrika, Germany, Switzerland) Ndi kuti, Ambuye?

Ndidzatsata,

Ndidzapita Naye, Naye konseko.

<sup>230</sup> Tsono, ndi mitu yanu yoweramitsa, kodi mudzapita naye kulilonse kumene Iye akutsogolereni? Mudzapita Naye pamene nthawi ikuchepa? Anthu akuzunza, kuseka kuseweretsa. Ndidzakhalabe ndi Iye, Ndidzapitabe. Ndidzayendabe ndi Inu, Ambuye kulikonse kumene Inu muli. Ndidzayimabe momvera ndi mowona. Ngati ndigwa, mudzandidzutsanso, Ambuye. "Iye amene ataya moyo wake chifukwa cha Ine adzaupeza!" Kotero ndinka Naye, Naye, konseko.

<sup>231</sup> Tsono, inu amene zikutanthauza chomwecho mu mitima yanu, tiyeni tikwezere manja anthu ndi mitima yathu kwa Iye tsopano.

Komwe Anditsogolera ndidzatsata,

Komwe Anditsogolera ndidzatsata,

Komwe Anditsogolera ndidzatsata,

Ndidzapita Naye, ndidzapita Naye.

Adzandipatsa chisomo ndi ulemerero,

Adzandipatsa . . .

Ambuye Yesu, uzirani tsono pa mipango iyi. Chiritsani odwala ndi ovutika awa, Ambuye. Tipatseni, Ambuye. Apatseni iwo machiritso, Ambuye, mu Dzina la Yesu.

Nadzapita nane, nane konseko.

<sup>232</sup> Mukumva bwino tsopano? Mukumva zonse zakonzeka tsopano? Ngati Iye . . . Lipenga la Ambuye lidzalira ndipo nthawi sidzakhalanso. Ndi Lipenga lotsirizalo tsono limenelo. Pamene mmawa udzafika kwa muyaya, kuwala, ndi kwabwino. Tiyeni tiyimbe tonse tsopano: Likaliratu lipenga la Ambuye. (Titsogolereni.)

<sup>233</sup> Tiyeni tikweza manja athu ndi kunena, "Mwa chisomo, Chanu, Ambuye." Mwa chisomo chanu, Ambuye! [Gulu libwereza - Mkonzi.] Tsono, ndife abale ndi alongo mwa Khristu. Tiyeni tingotembenuka ndi kugwirana dzanja ndi amene mwayandikana naye, nenani, "Ndi chithandizo cha Mulungu, pakwitana dzina langa kumeneko . . ."

<sup>234</sup> O, kodi imeneyo sidzakhalala nthawi? Kumangoyenda tsiku lina, kumangomva wina wake. "Ndi ndani? Amayi!"

“Sipatalinso tsopano.” Mu maminiti ochepa okha mwasinthika. Ndipo tidzakhala - kukomana nawo ndi kutengedwa pamodzi ndi iwo kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga. O, mwa kamphindi, mu kuthwanima kwa diso. Kunena, “Awa ndi M’bale Seward (M’bale wokalamba amene anali kukonda kukhala pa tchalichi pano.) Taonani, pano pali M’bale De Ark. Pano pali M’bale . . .Kotero - Bwanji, tawonani pano, onse angondizungilira. Chikuchitika ndi chiyani?” Mwangokhala mwa maminiti ochepa . . .“Ndikudziwa awonekera kwa ine. Sizikhala za patalinso tsopano; ndikusinthika tsopano, mu kamphindi.” O, inde! Pamene m’mawa udzadza, kwa muyaya, wowala ndi wabwino. Mitambo yonse yozizwitsa . . .

<sup>235</sup> Monga Iye anati, Israeli tsopano wakhala ngati mtambo wa m’mawa, nkhungu-Chilungamo chanu chachoka. Ndipo pamene zonse zathera mu Kuwala kwa Dzuwa limene limagwira zonsezo. (Amen!), kotero, dzina layitanidwa komweko, ndidzakhala komweko. Chabwino, mpaka usiku uno:

<sup>236</sup> Tiyeni tiimirire tsopano. O, kodi si chodabwitsa? Awa ndi malo a mwambamwamba ndi Khristu Yesu. Siungasinthanitse chimenechi ndi china chirichonse. Mukudziwa m’mene ndimakondera kusodza, ndi m’mene ndimakondera kusaka, chifukwa ndimamuona Mulungu m’chipululu m’menemo; ndimakonda choncho. Koma O, sindikanakhoza kusintha miniti imodzi ndi ichi pa zochitikazo . . .? . . .miniti imodzi ya ichi ndi yondikwanira.

<sup>237</sup> “Mulungu, mulenge mwa ine chitsitsimutso. Lolani ine ndikhale chitsitsimutso. Lolani wina aliyense wa ife akhale chitsitsimutsocho, chitsitsimutso mwa ine. Mundipangitse ine, Ambuye, kumva njala, mundipangitse ine kumva ludzu. Mulenge mwa ine Ambuye, chimene chikusowa mwa ine. Ndiloleni kuyambira ora lino kupita mtsogolomu ndikhale wantchito wanu wodzipereka, wantchito wabwino, wodalitsika kwambiri ndi Inu, wokhoza kwambiri, wodzichepetsa kwambiri, wachifundo chambiri, wofunitsitsa kugwira ntchito, woyang’anitsitsa pa zinthu zomwe ziri zoyenera ndi kuyiwala zinthu zimene ziri za mbuyo ndi zosayenera. Ndiloleni ndilimbikire kukafika pa malo apamwamba a kuitana kwa Khristu.” Amen! Kumeneko ndiko kukhumba kwathu, si choncho?

Chabwino, tiyeni - mpaka tikomananso usiku uno, tiyeni titenge Dzina la Yesu tsopano, yense wa inu tsopano.

Pita ndi Dzina la Yesu,  
Mwana wosauka ndi watsoka;  
Lidzakupatsa chimwemwe ndi chitonthozo,  
Pita nalo konseko.

Dzina lopambana, lokoma zedi!  
Chiyembekezero cha pansi, ndi chimwemwe  
chakumwamba;  
Dzina lopambana, lokoma zedi!  
Chiyembekezero cha pansi, ndi chimwemwe  
chakumwamba.

Tsopano tiyeni tiweramitse mitu yathu.

Pita ndi Dzina la Yesu,  
Ngati chishango pa zovuta;  
Pamene mayesero akuzinga,  
Puma Dzina loyeralo mwa pemphero . . .





*KUZINDIKIRA TSIKU LANU NDI UTHENGA WAKE* CHA64-0726M  
(Recognizing Your Day And Its Message)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu m'mawa pa 26 Julaye, 1964, ku Branham Tabernacle, Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2015 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)